# NTHANO YA YESU



Gawo 1

"Proclaiming Christ through the printed word"

BPH

Baptist Publishing House

OF THE BAPTIST MISSION OF ZAMBIA

P.O.BOX 1995 LUSAKA

~~ATH-ZM~~ VZM-ATH
Yenja

# NTHANO YA YESU

Gawo

THE STORY OF JESUS, Part I:
A STUDY OF GOSPEL OF MARK
(Nyanja)
First Published in Zambia
January 1, 1973 by
The Baptist Publishing House of
the Baptist Mission of Zambia
P. O. Box 1995
LUSAKA, ZAMBIA

Koma Yesu anali munthu wabwino. Anafa cifukwa ca macimo athu, monga m'mene mau a pamtima anenera, "Amene anasenza macimo athu mwini yekha m'thupi mwace pamtanda, kuti ife, titafa kumacimo, tikhale ndi moyo kutsata cilungamo."

### CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

(1) Yesu anapatsidwa mulandu wonama. Atsogoleri acipembedzo anapanga zinthu zomupatsilamo mulandu. Anafuna compheramo iye.

(2) Ali yense anamukana Yesu pamene anali kuzengedwa mandu ndi pamene anaphedwa. Asanafe, anakanidwa ndi kusekedwa.

(3) Yesu anafera macimo athu. Anafa kuti tipulumutsidwe ndi kuti macimo athu akhululukidwe.

### ZA INU

Yangananinso pa mutu waphunziro lathu. Ikani inde kapena iai ku mbali kwa mafunsowa.

Kodi mukhulupirira kuti Yesu Kristu ndi mwana wa Mulungu?
Kodi munamulandira iye kukhala Mpulumutsi wanu?
Kodi mulidi otsatira a Yesu Kristu?
Kodi mphamvu ya Yesu imalamulira moyo wanu?
Kodi cipembedzo canu ndi codzaza ndi moyo?

Lembani m'mene maphunzirowa akuthandizirani inu kukhala munthu wabwino. Ici cidzakuthandizani inu kukumbukira zimene munaphunzira. Ndipo muyenera kukhala monga momwe Yesu anatiphunzitsa ife.

### ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | |
|---|---|
| Lolemba | Luka 9:57-62 |
| Laciwiri | Luka 10:25-37 |
| Lacitatu | Luka 10:38-42 |
| Lacinai | Luka 11:1-13 |
| Lacisanu | Luka 12:22-31 |
| Loweluka | Yohane 3:14-21 |
| Lamulungu | Luka 14:25-53 |

ansembe anang'amba zobvala zace. Onse oweruza anamvomerezana kuti Yesu anayenera kufa.

Ndipo ena a anthu anayamba kumucita cipongwe Yesu. Anamthira malobvu. Ena anali kumumenya pamene anamseka maso. Anati "Ndani anakumenya nthawi ija; iwe mneneri? (ndime 65).

Kodi anthu anamseka bwanji Yesu pamene anali kufa? Werengani kuti muone.

MARKO 15:24-27

*Ndipo anampacika Iye, nagawana zobvala zace mwa iwo okha, ndi kucita maere pa izo, kuti adziwe yense adzatenga ciani. Ndipo panali ora lacitatu, ndipo anampacika Iye. Ndipo lembo la mlandu wace linalembedwa pa mwamba, MFUMU YA AYUDA. Ndipo anapacika pamodzi ndi Iye acifwamba awiri; mmodzi ku dzanja lace lamanja ndi wina kulamanzere.*

Pilato anamufunsa Yesu ngati anali mfumu ya Ayuda (ndime 2). Ankhondo anamuseka Yesu, namucha iye mfumu ya Ayuda (ndime 18). Pilato anaikapo cikhwangwani pamtanda MFUMU YA AYUDA. Cikhwangwani cinasonyeza anthu mulandu umene Yesu anapacikidwira. Cikhwangwanici cinamusekanso Yesu.

Kupha anthu ndi kupacika pamtanda inali imfa ya nkhanza ya ciroma. Inali ya anthu amene sanali kumvera malamulo. Yesu sanali wosamvera malamulo. Koma iwo anamuyesa iye monga m'modzi.

Ankhondo anamukhomera Yesu pamtanda panthawi ya ora lacisanu ndi cinai m'mawa. Anapanga maere kamba ka zobvala zace pamene iye anali kufa. Anafa ndi nthawi ya ora lacitatu m'madzulo.

Anayesetsa kumpanga Yesu kuoneka monga mbala. Anaphanso mbala ziwiri pamtanda. Anthu amene analinkudutsa anali kuganiza kuti Yesu anali woipa monga mbalazo.



ZA M'KATIMU

Mau Oyamba


| Mutu | | Tsamba |
|---|---|---|
| 1 | CIYAMBI CA UTHENGA WABWINO...... | 1 |
| 2 | KODI CIPHUNZITSO CATSOPANO NDI CIANI? ..................... | 5 |
| 3 | M'MENE ANTHU AMUGANIZIRIRA YESU........................... | 9 |
| 4 | ANTHU SAMVETSETSA YESU.......... | 13 |
| 5 | KODI UFUMU WA MULUNGU NDI CIANI?......................... | 17 |
| 6 | MPHAMVU YAIKURU YA YESU......... | 21 |
| 7 | MAKHALIDWE ABWINO A OPHUNZIRA... | 26 |
| 8 | PAMENE CIPEMBEDZO NDI COFUNIKA.. | 30 |
| 9 | KODI PAYENERA KUPEREKEDWA CIANI POOMBOLEDWA?.................... | 34 |
| 10 | KODI PAYENERA KUPEREKEDWA CIANI KUKHALA OPHUNZIRA?............. | 38 |
| 11 | MPHAMVU ZA YESU................ | 42 |
| 12 | YESU AKONZEKERA IMFA YACE....... | 46 |
| 13 | YESU AKANIDWA NDI KUPACIKIDWA PA MTANDA......................... | 50 |

*Nciani ici cimene awa alikucitira mboni? Koma anakhala cete, osayankha kanthu. Mkulu wa ansembe anamfunsanso, nanena naye, Kodi Iwe ndiwe Kristu, Mwana wace wa Wolemekezeka? Ndipo Yesu anati, Ndine amene; ndipo mudzaona Mwana wa munthu alikukhala ku dzanja lamanja la mphamvu, ndi kudza ndi mitambo ya kumwamba. Ndipo mkulu wa ansembe anang'amba maraya ace, nanena, Tifunirranjinso mboni zina? Mwamva mwano wace; muyesa bwanji? Ndipo onse anamtsutsa Iye kuti ayenera kufa. Ndipo ena anayamba kumthira malobvu Iye ndi kuphimba nkhope yace ndi kumbwanyula, ndi kunena naye Lota; ndipo anyamatawo anampanda Iye kofu.*

Yesu anali pa mulandu patsogolo pa onse atsogoleri acipembedzo (ndime 53). Panalibe amene anamuimilira Yesu. Angakhale Petro anamkana Iye (ndime 54).

Atsogoleri acipembedzo anayesayesa kupeza mboni kuti ziname ndi kuti amupatse mlandu Yesu. Iwo anali kufunilamo cifukwa comuphera Yesu. Munthu asanaweruzidwe kuti ayenera kufa, amboni awiri ayenera kulankhula zinthu zofanana. Ambiri anamupatsa mlandu Yesu. Koma mwa mbonizo panalibe zimene zinkanena zinthu zofanana.

Mboni imodzi inamupatsa mulandu Yesu kuti adati adzaononga kacisi ndi kumanganso m'masiku atatu (Onani Yohane 2:19). Yesu anali kulankhula za kuuka kwace kwa akufa.

Wansembe wamkulu amene anali kutsogolera mlanduwo anakalipa. Yesu sanali kuyankha zinthu zimene amboni anali kuzinena. Panalibe umboni wakuti iye anayenera kufa. Ndipo wa mkulu wansembe anamupangitsa Yesu kuti alankhule cinthu cimene cinkamupatsa iye mwini mlandu. Anamfunsa Yesu ngati anali mwana wa Mulungu. Yesu adayankha kuti "Inde."

Tsopano wansembe wa mkulu anali ndi cifukwa comphera Yesu. Anamupasa mlandu Yesu wocitira Mulungu mwano. Pamene munthu anali ndi mlandu wocitira mwano Mulungu, mkulu wa

MUTU 13

# YESU AKANIDWA NDI KUPACIKIDWA PA MTANDA

MAU A MULUNGU: Marko 14:43 mpaka 15:41

MAU A PAMTIMA: *"Amene anasenza macimo athu mwini yekha m'thupi mwace pamtanda, kuti ife, titafa kumacimo, tikhale ndi moyo kutsata cilungamo..."*
*1 Petro 2:24*

## CIDZIWITSO

Kukanidwa citanthauza kusiyidwa wekha. Citanthauza kuti palibe woyimilira ndi ife. M'phunziro lathu ophunzira a Yesu anamukana iye pamene anali kukonzekera imfa yace (Marko 14:50).

Phunziroli linena za Yesu alinkukanidwa, kusekedwa ndi kuphedwa. Anthu ambiri anaganiza kuti Yesu analephera cifukwa anaphedwa. Koma imfa yace inakwaniritsa cifukwa cimene anabwerera pa dziko pano. Anafa kuti ife tipulumuke.

Werengani ndimezi ndipo lembani mzere kunsi kwa maina a amene anamneneza Yesu.

## MARKO 14:55-65

*Ndipo ansembe akuru ndi akuru a milandu onse anafunafuna umboni wakutsutsa nao Yesu kuti amuphe Iye; koma sanaupeza. Pakuti ambiri anamcitira umboni wonama, ndipo umboni wao sunalingana. Ndipo ananyamukapo ena, namcitira umboni wakunama, nanena kuti, Ife tinamva Iye alikunena, kuti, Ine ndidzaononga Kacisi uyu wopangidwa ndi manja, ndi masiku atatu ndizamanga wina wosapangidwa ndi manja. Ndipo ngakhale momwemo umboni wao sunalingana. Ndipo mkulu wa ansembe ananyamuka pakati, namfunsa Yesu, nanena, Suyankha kanthu kodi?*

kuti cicitike, osati cifuniro cace.

Mulungu sankakhoza kutipulumutsa ife m'njira ina ili yonse. Yesu ankayenera kufa ndithu cifukwa ca ucimo wathu. Anali wokonzeka kufa.

Ndime 37-39. Pamene Yesu anabwerako, ophunzira ace anali m'tulo. Anawakalipira iwo. Anawafunsa kuti adzipemphera naonso. Anafunika kupemphera kuti apeze mphamvu yogonjetsera mayesero.

Ife tiri monga ophunzira a Yesu. Tiyenera kukhala ndi mphamvu, koma pamene mayesero abwera, tigwamo m'mayeserowo. Tiyenera kupemphera.

Ndime 39-41. Yesu anapempheranso. Ophunzira ace analinso m'tulo pamene iye anabweranso. Iye anati ankayenera kupitiliza kugona. Nthawi inapita yodikilira. Yuda, ophunzira amene anamugulitsa Yesu, analinkubwera (werengani ndime 42-50) Kodi Yuda anali yekha amene anamugulitsa Yesu (Onani ndime 50).

Yesu anabvutikadi. Analinso yekha. Ici cinampweteka mtima kwambiri. "Anadza kwa zace za iye yekha, ndipo ace a mwini yekha sanamulandire iye." (Yohane 1:11) Phunziro lathu limene libwera lidzanena za kupacikidwa pa mtanda kwa Yesu.

## ZA INU

Yesu anabvutika ndi kufera inu. Kodi muli okonzeka kuimirira ndi mphamvu cifukwa ca Ambuye? Kodi muli ndi mphamvu zokwanira kuti mungapikitsani ndi mayesero pamene akubwera pa inu? Kodi muli kudikira ndi kupemphera tsiku liri lonse?

## ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | |
|---|---|
| Lolemba | Luka 2:46-52 |
| Laciwiri | Luka 4:1-13 |
| Lacitatu | Luka 5:1-11 |
| Lacinai | Luka 6:1-12 |
| Lacisanu | Luka 7:11-23 |

Ndime 26. Atatsiriza kudya, Yesu ndi ophunzira ace anaturuka m'cipinda. Tiyeni tiwerenge zimene zinacitika.

MARKO 14:32-41

*Ndipo iwo anadza ku malo dzina lace Getsemane; ndipo ananena kwa ophunzira ace, Bakhalani pano, kufikira ndikapemphera. Ndipo anatenga pamodzi ndi Iye Petro, ndi Yakobo, ndi Yohane nayamba kudabwa kwambiri, ndi kusauka mtima ndithu. Ndipo ananena nao Moyo wanga uli wa cisoni cambiri, kufikira imfa. Bakhalani pano, nimudikhhire. Ndipo Iye anapita m'tsogolo pang'ono, nagwa pansi, napemphera kuti ngati nkutheka nthawi imene impitirire. Ndipo ananena, Abba, Atate, zinthu zonse zitheka ndi Inu; mundicotsere cikho ici; komatu si cimene ndifuna Ine, koma cimene mufuna Inu. Ndipo anadza nawapeza iwo ali m'tulo, nanena ndi Petro, Simoni, ugona kodi? unalibe mphamvu yakudikira ora limodzi kodi? Dikirani, pempherani, kuti mungalowe m'kuyesedwa; mzimutu uli wakufuna, koma thupi liri lolefuka. Ndipo anacokanso, napemphera, nanena mau omwewo. Ndipo anadzanso nawapeza ali m'tulu, pakuti maso ao analemeradi; ndipo sanadziwa comyankha Iye. Ndipo anadza kacitatu, nanena nao, Gonani tsopano, nimupumule; cakwanira; yafika nthawi; onani Mwana wa munthu aperekedwa m'manja a anthu ocimwa.*

Ndime 32 Yesu ndi ophunzira ace anapita ku Getsemane ku munda. Yesu anawafunsa iwo kuti amudikire pamene iye anali kupemphera.

Ndime 33-34. Yesu anatenga Petro, Yakobo ndi Yohane patsogoloko. Anawafunsa iwo kuti asagone pamodzi ndi iye. Yesu anali Mulungu ndi munthu. Anali wa umunthu ndiponso Mulungu. Mbari yace ya umunthu inali yolefuka.

Ndime 35-36. Ndipo Yesu anapitirirapo pang'ono napemphera. Anamufunsa Mulungu kuti amucotsere "cikho," ngati cinali cotheka. Cikho anali mabvuto ndi imfa zimene Yesu ankakomana nazo. Koma anafuna cifuniro ca Mulungu





# CIYAMBI CA UTHENGA WABWINO

**MAU A MULUNGU:** Marko 1:1-20

**MAU A PAMTIMA:** *"Ndipo ataperekedwa Yohane, Yesu anadza ku Galileya, nalalikira uthenga wabwino wa Mulungu, nanena, Nthawi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani uthenga wabwino."*
*Marko 1:14-15*

## CIDZIWITSO

Maphunziro athu pa miyezi itatu ikubwerayi azacokera m'buku la Marko. Amanena za Yesu. Tidzaphunzira za nchito yace. Anali mlaliki. Anaphunzitsa anthu zoonadi zocokera kwa Mulungu. Anacilitsanso odwala.

Phunziro ili limanena za m'mene anthu anayambira kumvera koyamba uthenga wabwino. Yohane anayamba kulalikira Yesu asanayambe. Yohane anawafunsa anthu kuti alape macimo awo. Anathandidza kupanga anthu kukhala eokonzekera Yesu. Ndipo Yesu nayensc analalikira uthenga umodzi modzi atabwera.

## ULALIKI WA YOHANE

Tiyeni tiwerenge ndimezi. Zimanena za munthu amene adayamba kulalikira Yesu asanayambe.

MARKO 1:1-8

*Ciyambi cace ca Uthenga Wabwino wa Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu. Monga mwalembedwa m'Yesaya mneneri, Ona, nditumа mthenga wanga, patsogolo pa nkhope yanu, Amene adzakonza*

*njira yanu; Mau a wopfuula m'cipululu, Konzani khwalala la Ambuye, Lungamitsani njira zace; Yohane anadza nabatiza m'cipululu, nalalikira ubatizo wa kutembenuka mtima wakuloza ku cikhululukiro ca macimo. Ndipo anaturuka a ku dziko lonse la Yudeya, ndi a ku Yerusalemu onse; nadza kwa iye nabatizidwa ndi iye muntsinje Yordano, poulula macimo ao. Ndipo Yohane anabvala ubweya wa ngamila, ndi lamba lacikopa m'cuuno mwace, nadya dzombe ndi uci wa kuthengo. Ndipo analalikira, kuti, Wondipambana ine mphamvu akudza pambuyo panga, sindiyenera kuwerama kumasula lamba la nsapato zace ine. Ndakubatizani inu ndi madzi; koma Iye adzakubatizani ndi Mzimu Woyera.*

Yohane amachedwa wopita patsogolo. Ncito yace inali kupita patsogolo pa Yesu ndi kuwaudza anthu kuti Ambuye anali kubwera.

Aneneri m'Cipangano Cakale ananena kuti Yohane adzabwera (Malaki 3:1) Yohane adzakhala mthenga wa Mulungu. Anakonzekeretsa anthu Yesu asanafike. Yohane anafuna kuti anthu akhale okonzeka kulandira Yesu ndi kukhulupirira mwa iye.

Yohane sanafune kuti Ayuda adzamuganizira kuti anali wamkuru monga Yesu. Werenganinso ndime 7. Nthawi zambiri munthu wa nchito ndiye amamasula lamba la nsapato. Yohane anati iye sanali woyenera konse kuti angamasule lamba la nsapato za Yesu.

Yohane anafunsa anthu kuti atembenuke. Pambuyo pace abatizidwe "monga kunena poyera kwa cifuniro cawo kucokako ku ucimo" (ndime 4 Mauthenga amoyo).

Anthu ambiri anamukhulupirira Yohane. Analapa macimo awo ndipo Yohane anawabatiza iwo kusonyeza kuti miyoyo yao inasinthika. Ubatizo wa Yohane unali wa madzi. Sukanapulumutsa anthu kapena kusintha miyoyo yao. Ubatizo siutipulumutsa ife lero. Ubatizo wa madzi ndi cithunzithunzi cimene cisonyeza kusintha





*Ndipo pamene iwo anali kudya, Iye anatenga mkate, ndipo pamene adadalitsa ananyema, napereka kwa iwo, kuti, Tengani; thupi langa ndi ili. Ndipo anatenga cikho, ndipo pamene adayamika, anapereka kwa iwo; ndipo iwo onse anamweramo. Ndipo iye anati kwa iwo, Ici ndi mwazi wanga wa cipangano, wothiridwa cifukwa ca anthu ambiri. Ndithu ndinena nanu, Sindidzamwanso cipatso ca mpesa, kufikira tsiku lijalo, limene ndidzamwa ico catsopano mu Ufumu wa Mulungu.*

*Ndipo atayimba nyimbo, anaturuka, namuka ku phiri la Azitona.*

Paskha anali madyerero amene Ayuda anali kukhala nawo caka ciri conse. Anakhala alinkudya madyererowa kucokera nthawi imene Ahebri anacokera ku Aigupto (Eksodo 12:43-50). Madyererowa anawathandiza iwo kukumbukira m'mene Ambuye anawapulumutsira ku Aigupto.

Yesu ndi ophunzira ace anali kudya cakudya ca madyererowa pamodzi. Tsopano ife Akristu tiri ndi mgonero mwa Ambuye m'malo mwa Paskha. Mgonero wa Ambuye utithandiza ife kukumbukira imfa ya Yesu. Pamene tikhala ndi mgonero wa Ambuye m'chalichi, tingawayamikenso cifukwa ca cipulumutso.

Ndime 22 "Tengani, dyani, ili ndi thupi langa." Ici sicitanthaudza kuti mkate linali thupi la anthu, thupi la Yesu. Ici citanthauza kuti mkate linaimilira m'malo mwa thupi la Yesu.

Ndime 23-24. Pamene analinkumwera m'cikho vinyo anaimilira m'malo mwa mwazi wa Yesu, m'wothiridwa cifukwa ca anthu ambiri, kutsimikiza kumvana kwa tsopano pakati pa Mulungu ndi anthu."

Ndime 25. Iyi inali nthawi yosiridzira kuti Yesu akhalenso pamodzi pa cakudya ndi ophunzira ace asanafe.

MUTU 12

# YESU AKONZEKERA IMFA YACE

MAU A MULUNGU: **Marko 13:1 mpaka 14:42**

MAU A PAMTIMA: *"Ndipo ananena, Abba, Atate, zinthu zonse zitheka ndi Inu; mundicotsere cikho ici; komatu si cimene ndifuna Ine, koma cimene mufuna Inu."* *Marko 14:36*

## CIDZIWITSO

Zinthu ziri m'phunzilori zinacitika **kuta**khala kanthawi pang'ono kuti Yesu afe. Anadziwa kuti adzafa posacedwa.

**Phunziro lathali linali la adani a Yesu. M'phunziroli Yesu ali ndi ophunzira ace. Ndi abwenzi ace. Adzapitiridza nchito ya Yesu iye atafa. Yesu adzapitirila kutumikira kudzera mwa ophunzira ace. Pamene tiphunzira, tiyeni tione m'mene ophunzira analiridi wokonzekera imfa ya Yesu.**

## CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

**(1) Mugonero wa Ambuye utithandiza ife kukumbukira imfa ya Ambuye. Pamene tikudya mgonero wa Ambuye, tingathokozenso iwo potifera ife.**

**(2) Mbari ya umunthu ya Yesu inalibe mphamvu. Anapemphera pamene imfa inalinkubwera.**

**(3) Yesu anakomana ndi imfa yekha. Ophunzira sanaimilire ndi iye pamene adani ace anali kukomana naye.**

**Tsopano werengani ndimezi zimene zinena za mgonero wa Ambuye woyamba.**



**kumene kwacitika m'mitima yathu. Ubatizo usonyeza kuti Yesu alowa m'mitima yathu. Usonyeza kuti timvera Yesu. Ndi kunena poyera kuti timutsatira Yesu.**

## UBATIZO WA YESU NDI MAYESERO

**Tsopano werengani ndimezi zonena za ubatizo wa Yesu ndi mayesero.**

MARKO 1:9-13

*Ndipo kunali masiku omwewo, Yesu anadza kucokera ku Nazarete wa ku Galileya, nabatizidwa ndi Yohane m'Yordano. Ndipo pomwepo, alimkukwera poturuka m'madzi, anaona Iye thambo litang'ambika, ndi Mzimu alikutsikira pa Iye monga nkhunda: ndipo mau anaturuka m'thambo, Mwana wanga wokondedwa ndiwe, mwa Iwe ndikondwera bwino. Ndipo pomwepo Mzimu anamkangamiza kunka kucipululu. Ndipo anakhala m'cipululu masiku makumi anai woyesedwa ndi Satana; nakhala ndi zirombo, ndipo angelo anamtumikira.*

**Yohane anali kubatiza anthu amene anatembenuka. Yesu sanafunika kutembenuka. Cifukwa analibe macimo. Koma anamufunsa Yohane kuti amubatizebe.**

**Yesu anatipatsa ife citsanzo pamene anabatizidwa. Afuna kuti ife tibatizidwe pamene tapulumutsidwa. Ife amene tiri Akristu tinabatizidwa, monga m'mene anabatizidwira.**

**Ubatizo wa Yesu unali monga cithunzithunzi. Pamene anali kulowa m'madzi, anaonetsa imfa yace ndi kuikidwa m'manda kwace. Pamene anaturuka m'madzi, anaonetsa kuuka kwa akufa.**

**Mau ocokera ku mwamba (ndime 11) anaonetsa kuti Mulungu anakondwera ndi ubatizo wa Yesu. Mau anali Mzimu Woyera. Mzimu Woyera analinso ndi Yesu m'nchito yace.**

**Atabatizidwa Yesu, satana anamuyesa iye. Ici cinali ciyeso ca Yesu (werengani Luka 4:1-13 kuti muone m'mene Yesu anapambanira Satana).**

Satana atiyesanso ife. Pamene tifuna kuti tikhalire Ambuye, Satana afuna kutiononga ife. Koma Ambuye atipatsa mphamvu. Ife tikhodza kugonjetsa Satana, monga m'mene Yesu anacitira.

CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

(1) Uthenga wa Yesu Kristu ndi uthenga wabwino. Aneneri am'nthawi ya Cipangano Cakale ananena za kubwera kwa Yesu. Ananenanso za kubwera kwa Yohane.

(2) Yohane analalikira ndipo anawafunsa anthu kuti atembenuke. Anawafunsa anthu kukonzekera kubwera kwa Yesu. Yohane anali wopita patsogolo.

(3) Yohane anabatiza anthu amene anatembenuka. Yesu sanafunika kutembenuka. Komabe anamufunsa Yohane kuti amubatize. Mulungu anakondwera ndi ubatizo wa Yesu.

(4) Yesu atabatizidwa, Satana anafunitsitsa kuti iye alakwe. Satana amatiyesanso ife lero, pamene tifuna kumukondweretsa Mulungu.

ZA INU

Kodi inu mukhulupirira za uthenga wabwino wa Yesu? Kodi inu munamulandira Yesu kukhala Mpulumutsi wanu?

Satana adzacipangitsa kukhala cinthu cobvuta kuti inu mumutsatire Yesu m'moyo wanu. Koma Ambuye adzakuthandizani inu. Adzakupatsani mphamvu zopambanira mayesero. Adzakuthandizani inu kukhala bwino.



Yesu anali kutanthaudza kuti boma liri ndi mphamvu pa ife. Tiyenera kukhoma msonkho ndi kumvera malamulo. Ena alinso ndi mphamvu pa ife. Tiyenera kuwalemekeza ndi kuwamvera iwo.

Koma Ambuye Mulungu ali ndi mphamvu pa zonse ndi ife. Tiyenera kuona kuti mphamvu zao zitilamulira ife.

CIMENE PHUNZILORI LIMATIUZA IFE

(1) Tiyenera kudziwa kuti boma liri ndi mphamvu pa ife. Tiyenera kulimvera boma. Sitiyenera kumenyana ndi ulamuliro wa boma.

(2) Ambuye ali ndi udindo kukhala ndi mphamvu pa zinthu zonse ndi anthu onse.

(3) Sitiyenera kulola zizolowezi kapena miyambo, monga kumwa mowa, kuti zitilamulire ife. Tiyenera kulola Ambuye kutilamulira ife masiku onse.

ZA INU

Kodi Ambuye alamulira moyo wanu? Ngati mulola kumwa mowa kapena zizolowezi zina zoipa kulamulira moyo wanu, simuli pansi pa ulamuliro wa Ambuye.

Ngati simunali kulola Ambuye kulamulira moyo wanu, yambani tsopano. Ambuye angagwiritse nchito moyo wanu mu nchito yao.

ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | |
|---|---|
| Lolemba: | Aroma 11:29-36 |
| Laciwiri: | Aroma 12:1-8 |
| Lacitatu | Aroma 13:1-10 |
| Lacinai | Aroma 15:1-17 |
| Lacisanu | Aroma 14:1-9 |
| Loweluka | Luka 21:1-4 |
| Lamulungu: | Luka 1:67-80 |

anthu. Werenganinso ndime 31-32 kuti muone m'mene ansembe, alembi ndi ena anamuyankhira Yesu.

Ngati anthuwo anati mphamvu za Yohane inacokera kwa Mulungu, anadziweruza iwo wokha pakuti sanamukhulupirire. Ndiponso anayenera kumvomerezanso kuti mphamvu ya Yesu inacokeransokwa Mulungu. Pezani mu ndime 32 cimene cikadaoneka ngati anati mphamvu ya Yohane siinacokere kwa Mulungu.

Kodi ansembe, alembi ndi ena anali kuopa anthu amene anakhulupirira mwa Yohane? Anamuyankha bwanji Yesu? Kodi anali kufuna kuti mphamvu ya Yesu ilamulire miyoyo yao?

ANTHU AMENE ANAFUNA KUNYENGA YESU

Afarisi anali aphunzitsi acipembedzo. Aherode anali anthu amene anali kuphunzitsa anthu kuti munthu wina wa m'banja la Herode anayenera kulamulira m'malo molamulidwa ndi bwana mkubwa waciroma.

Nthawi zambiri Afarisi ndi Aherode anali wodana. Nthawiyi anapitira limodzi kukayesa kumuputsitsa Yesu. Anayamba ndi kukometsa pa kamwa ndithu. Anati Yesu anali okhulupirika ndipo samakonda ena ndi kuda ena (ndime 14).

Ndipo anamfunsa Iye ngati cinali cabwino kukhoma msonkho kwa mkuru wolamulira Waciroma. Uwu unali msonkho wa nyumba. (Analinso ndi msonkho wa nthaka ndipo msonkho wa ndalama zimene anali kupata).

Yesu anadziwa kuti anali kufuna kumunyenga iye. Anawafunsa kuti amusonyeze rupiya. Pamene anafunsa kuti n'cithunzithunzi ca ndani cinalipo, anati ca Kaisara.

"Perekani zace za Kaisara kwa Kaisara, ndi zace za Mulungu kwa Mulungu." (ndime 17) Yesu anawauza. Yankho lace linawadabwitsa iwo. Sanadziwe conena.





# KODI CIPHUNZITSO CATSOPANO NDI CIANI?

MAU A MULUNGU: Marko 1:21-45

MAU A PAMTIMA: *"Ndipo Yesu anayendayenda m'mizinda yonse ndi m'midzi, namaphunzitsa m'masunagoge mwao, nalalikira uthenga wabwino wa Ufumuwo, naciritsa nthenda iri yonse ndi zofoka."*
*Mateyu 9:35*

CIDZIWITSO

Sabata yatha tinaphunzira kuti nchito ya Yesu inali yolalikira, kuphunzitsa, ndi kuciritsa anthu odwala. Nthawi zina amacita zinthu zitatuzi panthawi imodzi. Pamene Yesu amaciritsa anthu odwala, anali kuphunzitsa ndi kulalikira za cikondi ca Mulungu. Yesu anaciritsa anthu cifukwa anawakonda iwo.

M'phunziroli tiona kuti Yesu anali kuphunzitsa ndi mphamvu zapadera. Anthu anadabwa, koma anali wokondwa kumvera iye pamene anali kuphunzitsa ndi kulalikira.

CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

(1) Yesu sanaphunzitse cinthu cacilendo. Iye anaphunzitsa zoonadi zakale zocokera kwa Mulungu. Aneneri anaphunzitsa zoonadi zimenezi mu nthawi ya Cipangano Cakale. Koma Yesu anali kuphunzitsa ndi mphamvu zapadera.

(2) Yesu anaciritsa anthu cifukwa anawakonda iwo. Anafuna kuwathandiza. Anabwera m'dziko muno kudzatumikira.

(3) Yesu sanasamaleko mwambo wa Ayuda. Anali kuthandiza anthu amene anali kufuna

cithandizo, kuli konse kumene anali.

Mphamvu mukuphunzitsa. Tiyeni tiwerenge ndimezi. Kodi ndi cifukwa ciani anthu anali kumvetsera Yesu?

MARKO 1:21-22

*Ndipo iwo analowa m'Kapernao; ndipo pomwepo pa dzuwa la Sabata iye analowa m'sunagoge naphunzitsa. Ndipo anazizwa ndi ciphunzitso cace; pakuti anaphunzitsa monga mwini mphamvu, si monga alembi.*

Kodi munacipeza cifukwa cimene anthu anamvetsera pamene Yesu anali kulalikira? Kodi anakonda kumvera mphunzitsi amene: anali kulankhula ndi mphamvu ya padera?

Yesu anali wamthenga woyamba wocokera kwa Mulungu (kucotsapo Yohane) kucokera nthawi ya Cipangano Cakale yitatha, kukwanira zaka madzana anai. Patsiku la sabata Yesu anapita ku sunagoge (Malo a Ayuda opemphererako). Uwu unali mwambo wace. Ophunzira ace anapita ndi Iye. Yesu analalikira m'sunagoge ndi kuphunzitsa anthu. Nthawi zina amaciritsa anthu m'menemo.

Aphunzitsi Aciyuda a nthawi imeneyo anafunitsitsa kusonyeza kuti zonse zimene anali kunena zinali zoona. Yesu sanafune kusonyeza anthu kuti zimene anali kunena zinali zoona.

Yesu anali ndi mphamvu kucokera kwa Mulungu. Anthu anali wokondwa kumva Yesu cifukwa anali kulankhula ndi mphamvu zapadera.

ULAMULIRO PA MIZIMU YONYANSA

Werengani ndime izi. Ndi cifukwa ciani anthu anadabwa ndi cimene Yesu anacita?

MARKO 1:23-28

*Ndipo pomwepo panali munthu m'sunagoge mwao ali ndi mzimu wonyansa; ndipo anapfuula*



MARKO 11:27-33

*Ndipo iwo anadzanso ku Yerusalemu; ndipo m'mene Iye anali kuyenda m'Kacisi, anafika kwa Iye ansembe akuru, ndi alembi ndi akuru; nanena naye, Izi muzicita ndi ulamuliro wotani? Kapena anakupatsani ndani ulamuliro uwu wakucita izi? Ndipo Yesu anati kwa iwo, Ndikufunsani mau amodzi, mundiyankhe ine, ndipo ndidzakuuzani ulamuliro umene ndicita nao zinthu zimenezi. Ubatizo wa Yohane ucokera Kumwamba kodi, kapena kwa anthu? Mundiyankhe. Ndipo anatsutsana mwa iwo okha, nanena, Tikati, Kumwamba; adzanena Iye, Ndipo simunakhulupirira iye bwanji? Koma tikati, kwa anthu anaopa anthuwo; pakuti onse anamuyesa Yohane mneneri, ndithu. Ndipo iwo anamyankha Yesu, nanena, Sitidziwa. Ndipo Yesu ananena nao, Inenso sindikuuzani ulamuliro umene ndicita nao zinthu zimenezi.*

MARKO 12:13-17

*Ndipo anatuma kwa iye ena a Afarisi ndi a Aherode, kuti akamkole Iye m'kulankhula kwace. Ndipo pamene anafika, ananena naye, Mphunzitsi, tidziwa kuti muli woona ndipo simusamala munthu; pakuti simuyang'ana nkhope ya anthu, koma muphunzitsa njira ya Mulungu moona nkuloleka kodi kupereka msonkho kwa Kaisara, kapena iai? Kodi tipereke kapena tisapereke? Koma Iye anadziwa cinyengo cao, nati kwa iwo, Mundiyeseranji? Nditengereni rupiya latheka, kuti ndilione. Ndipo analitenga. Ndipo ananena nao, Cithunzithunzi ici, ndi cilembo cace ziri za yani? Ndipo anati kwa Iye, Za Kaisara. Ndipo Yesu anati kwa iwo, Perekani zace za Kaisara kwa Kaisara, ndi zace za Mulungu kwa Mulungu. Ndipo anazizwa naye kwambiri.*

Kodi Yesu anawayankha bwanji akuru akuru ndi alembi ndi ena? Taonaninso ndime 29. Yesu anayankha funso pofunsa funso!

Yesu anafunsa ngati mphamvu ya Yohane kuti abatize inacokera kwa Mulungu kapena kwa

MUTU 11

## MPHAMVU ZA YESU

MAU A MULUNGU: Marko 11-12

MAU A PAMTIMA: *"Mphamvu zonse zapatsidwa kwa ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi."*
*Mateyu 28:18*

### CIDZIWITSO

Mphamvu citanthauza udindo kapena kudzi-letsa. Anthu ali ndi mphamvu pa anzao. Angauze anzao cimene ayenera kucicita. Ena ali ndi mphamvu zambiri zoposa zimene ena ali nazo. Makolo ali ndi mphamvu pa ana ao pamene anawo ali ang'ono.

Phunziro lathu linena za mphamvu za Yesu. Tisanayambe kuphunzira phunziroli, onani mau a pamtima. Kodi ndimeyi ikuti Yesu ali ndi mphamvu zotani?

### ANTHU AMENE ANAFUNSA ZA MPHAMVU ZA YESU

Mu Marko 11:11-14 Yesu anaona mtengo wa mkuyu umene sunali kubala zipatso. Anati m'mau a masiku awo, "Munthu sadzadyanso zipatso zako nthawi zonse." Sanenene cifukwa cimene analankhulira tere.

Ndime 15-17 zitiuza ife za m'mene anathamangitsira wosintha ndalama m'Kacisi. Ndipo Yesu anaphunzitsa cikhulupiriro ndi kukhululukira mu ndime 22-26.

Ansembe akuru ndi alembi anamfunsa Yesu kuti zinali mphamvu zotani zocitira zinthu zotere. Werengani kuti mupeze yankho.



*iye kuti, Tiri ndi ciani ife ndi Inu Yesu wa ku Nazarete? Kodi mwadza kudzationonga ife? Ndikudziwani, ndi Woyerayo wa Mulungu. Ndipo Yesu anaudzudzula, kuti, Khala uli cete, nuturuke mwa iye. Ndipo mzimu wonyansa, pomng'amba, ndi kupfuula ndi mau akuru, unaturuka mwa iye. Ndipo anazizwa onse, kotero kuti anafunsana mwa iwo okha, kuti, Ici nciani? ciphunzitso catsopano! ndi mphamvu alamula ingakhale mizimu yonyansa, ndipo imvera Iye. Ndipo mbiri yace inabuka pompaja ku dziko lonse la Galileya lozungulirapo.*

Kodi munaipeza mphamvu ya padera m'ndimezi? Yesu anali ndi ulamuliro pa mizimu yonyansa, monga aanalalikira ndi kuphunzitsira ndi mphamvu zapadera. Angakhale munthu amene anali ndi mzimu wonyansa anadziwa kuti Yesu sanali muphunzitsi wamba ai. Anadziwa kuti Yesu anali wocokera kwa Mulungu anaona kuti Yesu anadza kudzamulanga iye.

Yesu anaulamulira mzimu wonyansa kuti ucoke mwa munthu uja. Pambuyo pace maganizo a munthuyo analinso omasuka. Munthu uja anapangika kukhala bwino. Onse anadabwa. Anaona kuti Yesu ali ndi ulamuliro pa mizimu yonyansa. Nkhani yonena za mphamvu ya padera ya Yesu inapita msanga.

### ULAMULIRO PA KUCIRITSA

Tiyeni tiwerenge ndimezi. Kodi ndi cifukwa ciani anthu ambiri anamva kuti Yesu anali kuciritsa anthu?

MARKO 1:29-34

*Ndipo pomwepo, poturuka m'sunagoge, iwo analowa m'nyumba ya Simoni ndi Andreya pamodzi ndi Yakobo ndi Yohane. Ndipo mpongozi wace wa Simoni anali gone wodwala malungo; ndipo pomwepo anamuuza za iye: ndipo anadza namgwira dzanja, namuutsa; ndipo malungo anamleka, ndipo anawatumikira iwo.*

*Ndipo madzulo, litalowa dzuwa, anadza nao kwa Iye onse akudwala, ndi akugwidwa ndi ziwanda. Ndipo mudzi wonse unasonkhana pakhomo. Ndipo anaciritsa anthu ambiri akudwala nthenda za mitundu mitundu, naturutsa ziwanda zambiri; ndipo sanalola ziwandazo zilankhule, cifukwa zinamdziwa Iye.*

Yesu anaonetsa ulamuliro wace m'sunagoge ndi zimene anaphunzitsa. Anawonetsa ulamuliro wace pamene anaturutsa mzimu wonyansa mwa munthu uja. Ndipo Yesu anapita kunyumba kwa Petro. Apongozi ace a Petro anali wodwala ndi malungo. Yesu anawaciritsa. Malungo amene amapangitsa anthu kukhala opanda mphamvu kwa nthawi yaitali. Koma iwo ananyamuka nawaphikira cakudya. Yesu anawaciritsadi ndithu.

Anthu a m'tauniyo anamva kuti Yesu anali kuciritsa anthu. Anabweretsa ambiri odwala abale awo ndi abwenzi awo, ndi enanso amene anali ndi mizimu yonyansa. Yesu anawaciritsa, iwo.

## ZA INU

Yesu akuyang'anirani inu. Ali wa nkhawa ndi moyo wanu wa thupi, ndi moyo wanunso wa mzimu. Yesu ali wankhawa mu zinthu zonse za moyo wanu. Afuna kumuthandizani inu nthawi zonse.

Mungamukhulupirire Yesu. Sadzakuiwalani. Afuna kukhala mfumu ya moyo wanu. Afuna kukhala ndi ulamuliro pa moyo wanu. Kodi mudzamulola Yesu kukhala ndi ulamuliro pa moyo wanu?



atanthauzadi kuti tiyenera kufa cifukwa ca iye ngati tifuna kupulumutsidwa? Kodi tizazunzidwa? Kodi muli okonzeka kupereka mtengo okhalira ophunzira a Yesu?

## CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

(1) Mtengo wokhalira ophunzira wa Yesu ndi kumvera Ambuye m'zinthu zonse. Tiyenera kuyika Ambuye poyamba. Sitingalole ndalama ndi zinthu zina za m'dziko kucinjiriza njira yokhalira wophunzira weni weni.

(2) Tiyenera kukhala ndi zifukwa zoyenera zotsatira Ambuye. Tiyenera kuganizira za m'mene tingatumikire.

(3) Ambuye adzatidalitsa ife cifukwa tiwatsata iwo. Pamene tibvutika cifukwa ca kuti tiri Akristu, tidzakhalanso ndi ulemerero wace ndipo madalitso ace.

## ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | | |
|---|---|---|
| Lolemba: | | Aroma 3:19-31 |
| Laciwiri: | Aro | Aroma 5:1-10 |
| Lacitatu: | | Aroma 6:1-10 |
| Lacinai: | | Aroma 8:5-14 |
| Lacisanu: | | Aroma 8:28-39 |
| Loweluka: | | Luka 15:11-24 |
| Lamulungu: | | Aroma 10:1-9 |

waukuru ndithu kuupereka pokhala ophunzira.

Cuma cinatsekereza njira yomtsatira Yesu (ndime 23-27). Ayuda anaganiza kuti kukhala ndi cuma cinali cizindikiro ca madalitso a Mulungu. M'masiku amenewo, nthawi ili yonse Mulungu atadalitsa munthu, sanali kumupatsa cuma. Mulungu satipatsa cuma nthawi zonse monga madalitso.

Yesu anati cuma cinali kucinjiriza anthu kulowa kumwamba. Anati "amene akhulupirira cuma" (ndime 24) Sangalowe kumwamba. Anthu ena a cuma saganiza kuti awafuna Ambuye cifukwa akhulupirira cuma cao.

Anthu acuma ambiri ndi Akristu. Amatumikira ndalama zao m'njira yoyenera. Amatumikira ndalama zao pamene atumikira Ambuye.

Ife amene sitiri acuma tilola kuti zinthu zina ziticinjirize kulowa kumwamba ndi kukhala wophunzira a Yesu. Kodi mungazichule zina za zinthuzo?

Mtengo wakukhala wophunzira (ndime 28-31). Petro anali kuganiza kuti anapereka cinthu cacikuru pokhala womutsatira Yesu. "Onani, ife tinasiya zonse, ndipo tinakutsatani inu." (ndime 28)

Mu ndime 29-31 Yesu anamuudza Petro kuti ali yense amene anasiya zonse cifukwa ca iye ndi cifukwa ca uthenga wabwino akanadalitsidwa. Anatinso anthu otere akanazunzidwa cifukwa anali Akristu. Uwu ndiwo mtengo wa ophunzira Yesu. Mphotho m'dziko lobweraro idzakhala moyo wosatha (ndime 30)

Yesu anati anthu ambiri amene aganiza ali olemekezeka tsopano, adzakhala otsadziwika pothera. "Ndi akuthungo adzakhala oyamba."

ZA INU

Taonaninso pa mau a pamtima. Kodi anena mtengo wokhala wophunzira wa Yesu? Kodi Ambuye





## M'MENE ANTHU AMUGANIZIRIRA YESU

MAU A MULUNGU: Marko 2:1 mpaka 3:6

MAU A PAMTIMA: *"Pakuti mau a mtanda ali ndithu cinthu copusa kwa iwo akutayika, koma kwa ife amene tirikupulumutsidwa ali mphamvu ya Mulungu."*
*1 Akorinto 1;18*

### CIDZIWITSO

M'mene anthu amuganizirira Yesu citanthaudza cimene acita atakomana naye. M'phunziro lathu lapitali anthu anakonda zimene Yesu anali kulankhula ndi kuzicita. Ambiri anamukhulupirira iye namutsatira.

Phunziro ili linena za ena amene anamuganizira zotsutsana naye. Awa anali anthu akuru akuru acipembedzo caciyuda. Sanafune Yesu kukhala ndi mphamvu pa iwo. Anafuna kutsatira mwambo wa Ciyuda m'malo motsatira Yesu.

Tsopano pezani cifukwa cace cimene akuru akuru acipembedzo anatsutsana naye Yesu.

### MARKO 2:1-12

*Ndipo polowanso m'Kapernao atapita masiku ena, kunamveka kuti ali m'nyumba. Ndipo ambiri anaunjikana, kotero kuti anasowa malo, ngakhale pakhomo pomwe; ndipo analankhula nao mau. Ndipo anadza kwa iye otenga munthu wodwala manjenje, wonyamulidwa ndi anthu anai. Ndipo pamene sanakhoza kufika kuli iye, cifukwa ca khamu la anthu, anasasula chindwi pokhala Iye; ndipo pamene anatha kuliboola, anatsitsa mphasa m'mene alinkugonamo wodwala manjenjeyo. Ndipo Yesu pakuona cikhulupiriro cao ananena ndi wodwala manjenje, Mwana, macimo*

ako akhulukidwa. Koma anakhalapo ena a alembi akuganizira mumtima mwao, Munthu amene atero bwanji? acita mwano; akhoza ndani kukhululukira macimo, koma m'modzi, ndiye Mulungu? Ndipo pomwepo Yesu pozindikira mumtima mwace kuti alikuganizira comweco mwa iwo okha, ananena nao, Muganiza bwanji zinthu izi m'mitima yanu? Capafupi nciti, kapena kuuza wodwala manjenje kuti, Macimo ako akhululukidwa; kapena kuti, Nyamuka, senza mphasa yako, nuyende?' ~~Koma~~ kuti mudziwe kuti Mwana wa munthu ali mwini ulamuliro wakukhululukira macimo pa dziko lapansi (ananena ndi wodwala manjenje), Ndikuuza iwe, Nyamuka, senza mphasa yako, numuke kwanu. Ndipo ananyamuka iye pomwepo, nasenza mphasa, naturuka pamaso pa iwo onse; kotero kuti anadabwa onse, nalemekeza Mulungu, nanena kuti, Zotere sitinaziona ndi kale lonse.

Yesu anali kulalikira m'malo onse a mu Galileya. Ndipo anapita ku Kapernao, kulalikira ndi kuciritsa anthu.

Nkhani inamveka kuti Yesu anabweranso. Ambiri anabwera kunyumba kumene iye anali. Posacedwa nyumba inadzala.

Abwenzi anai anabweretsa munthu wodwala manjenje kwa Yesu kuti akaciritsidwe. Sakanakhodza kupyola mu ciunyinji ca anthuwo. Werengani ndime ya cinai kuti mupeze cimene anthu anaiwa anacita. Anamutengera munthu wodwalayo pa tsidwi. Anapanga zenje pa tsindwipo namutsitsira iye m'cipinda.

Pamene Yesu anaona cikhulupiriro cao, anacita ciani? Anamuuza munthu wodwalayo kuti macimo ace anakhulukidwa. Akuru akuru acipembedzo Caciyuda anakwiya. Sanakhulupirire kuti Yesu anali ndi mphamvu yokhululukira ucimo. Sanaganizire kuti Yesu anali mwana wa Mulungu.

Akuru akuru acipembedzo namupatsa mlandu wocita mwano. Anati Yesu anali kuyesa



mwana. Ndipo Yesu anamyang'ana, namkonda, nati, kwa iye, Cinthu cimodzi cikusowa: pita, gulitsa zonse uli nazo, nuzipereke kwa anthu aumphawi, ndipo cuma udzakhala naco m'mwamba; ndipo ukadze kuno, unditsate ine. Koma nkhope yace inagwa pa mau awa, ndipo anacoka iye wacisoni; pakuti anali mwini cuma cambiri. Ndipo Yesu anaunguzaunguza, nanena ndi ophunzira ace, Okhala naco cuma adzalowa mu Ufumu wa Mulungu ndi kubvuta nanga! Ndipo ophunzirawo anazizwa ndithu ndi mau ace. Koma Yesu anayankhanso nanena nao, Ananu, nkobvuta ndithu kwa iwo akutama cuma kulowa mu Ufumu wa Mulungu! Nkwa pafupi kuti ngamila ipyole diso la sinoano koposa kuti mwini cuma alowe mu Ufumu wa Mulungu. Ndipo anadabwa, nanena kwa iye, Ndipo angathe kupulumuka ndani? Yesu anawayang'ana iwo nati, Sikutheka ndi anthu, koma kutheka ndi Mulungu; pakuti zinthu zonse zitheka ndi Mulungu. Petro anayamba kunena naye, Onani, ife tinasiya zonse, ndipo tinakutsatani inu. Yesu anati, Ndinena ndi inu ndithu, Palibe munthu anasiya nyumba, kapena abale, kapena alongo, kapena amai, kapena atate, kapena ana, kapena minda, cifukwa ca ine, ndi cifukwa ca Uthenga Wabwinowo, amene sadzalandira makumi khumi tsopano nthawi yino, nyumba, ndi abale, ndi alongo, ndi amai, ndi ana, ndi minda, pamodzi ndi mazunzo; ndipo nthawi irinkudza moyo wosatha. Koma ambiri akuyamba adzakhala akuthungo, ndi akuthungo adzakhala oyamba.

Munthu amene anakana kukhala ophunzira wa Yesu (ndime 17-22). Munthu amene anabwera kwa Yesu alinkuthamanga nafuna kuti apulumutsidwe. Anagwada. Anamucha Yesu, Mphunzitsi. Munthuyo anadziwa kuti Yesu anali munthu wabwino. Anaganiza kuti angakhodze kupita kumwamba pokhala bwino ndi kucita zinthu zabwino. (Onani Mateyu 19:16)

Sanali munthu oipa. Anasunga malamulo. Anali wabwino kwa anthu. Koma Yesu anamufunsa iye, kucita koposa kukhala cabe bwino. Yesu anamufunsa iye kuti adzisiye ndalama zace zonse, namutsatire iye. Uwu unali mtengo

MUTU 10

## KODI PAYENERA KUPEREKEDWA CIANI KUKHALA OPHUNZIRA?

MAU A MULUNGU: Marko 10

MAU A PAMTIMA: *"Pakuti yense wakufuna kupulumutsa moyo wace adzautaya; ndipo yense wakutaya moyo wace cifukwa ca ine, ndi cifukwa ca Uthenga Wabwino, adzaupulumutsa."*
*Marko 8:35*

### CIDZIWITSO

Kukhala ophunzira citanthauza kukhala omutsatira Yesu Kristu. Ambiri a ife tifuna kukhala omutsatira Yesu. Koma kodi tifuna kupereka mtengo wace? Mtengo wokhalira womutsatira Yesu ndi kumvera Ambuye m'zinthu zonse.

Ndi nthawi yokhalira ophunzira a Yesu. Koma mtengo wace ndi waukurudi. Tiyenera kudzisiya zonse zoticinjiriza ife m'njira. Zingakhale ndalama, mphamvu, zifuno kudzikonda, nsanje, kudana, kapena zizolowezi zimene sitifuna kudzisiya.

Werengani ndimezi. Ndi ciani cinamulepheretsa munthuyo kukhala ophunzira?

### MARKO 10:17-31

*Ndipo pamene iye anaturuka kutsata njira, anamthamangira munthu, namgwadira iye, namfunsa, Mphunzitsi wabwino, ndidzacita ciani kuti ndilandire moyo wosatha? Ndipo Yesu anati kwa iye, Undicha ine wabwino bwanji? palibe wabwino koma mmodzi, ndiye Mulungu. Udziwa malamulo, Usaphe, Usacite cigololo, Usabe, Usacite umboni wakunama, Usanyenge, Lemekeza atate wako ndi amako. Ndipo iye anati kwa Iye, Mphunzitsi, zonsezi ndinazisunga kuyambira ndiri*



kutenga malo a Mulungu. Sanakhulupirire kuti Yesu akanakhululukira macimo a munthu wodwala. Anati Yesu anali kufuna cabe kuti achedwe mwana wa Mulungu.

Yesu anamufunsa munthu uja kuti anyamuke nayende. Munthuyo anayenda ndipo anali bwino. Ali yense anaona kuti anacilitsidwadi. Werengani ndime 12 kuti mupeze cimene anthu anacita. Anamulemekeza Mulungu. Tiyeni tiwerenge ndimezi kuti tione m'mene akuru akuru acipembedzo anali kutsutsirana naye Yesu.

### MARKO 2:15-17

*Ndipo ananyamuka namtsata Iye. Ndipo kunali kuti anakhala pakudya m'nyumba mwace, ndipo amisonkho ndi ocimwa ambiri anakhala pansi pamodzi ndi Yesu ndi ophunzira ace, pakuti anali ambiri, ndipo anamtsata Iye. Ndipo alembi a kwa Afarisi, pakuona kuti alinkudya nao ocimwa ndi amisonkho, ananena ndi ophunzira ace, Uyu akudya ndi kumwa nao amisonkho ndi ocimwa. Ndipo pamene Yesu anamva ici, ananena nao, Akulimba safuna sing'anga, koma odwala ndiwo; sindinadza kudzaitana olungama, koma ocimwa.*

Ndime 13-14 zinena za Yesu pamene anali kuitanira Levi kuti akhale ophunzira. Anali wokhometsa msonkho.

Mateyu atakhala omutsatira Yesu, anakonza madyerero kuyumba kwace. Anaitana Yesu ndi ophunzira ace. Mateyu anaitana wokhometsa msonkho ambiri ndi wocimwa kuti akamudziwe Ambuye.

Kodi akuru akuru acipembedzo ananena ciani pamene anaona Yesu anali kudya pamodzi ndi anthu otero? Werengani ndime 16. Anaganiza kuti Yesu sangadye pamodzi ndi anthu amene sanali kutsatira malamulo awo.

Pamene Yesu anamva alinkudandaula, anati "Anthu amene ali bwino safuna sing'anga,

koma amene ali wodwala. Sindinadza kudzaitana olungama, koma ocimwa." (ndime 17)

Yesu anali kutanthaudza kuti akuru akuru Aciyuda amene anali kudziganizira kuti anali olungama sanali olungama konse. Iwo anayenera kumulandira Yesu ndi kumvera Iye. Pamene iwo akanabvomereza kuti anali wocimwa, Mulungu akanawakhululukira.

## CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

(1) Anthu ambiri anamutsatira Yesu. Anakhulupirira zimene analalikira. Anali wokondwera pamene anaciritsa anthu odwala.

(2) Akuru akuru acipembedzo caciyuda sanamutsatire Yesu. Iwo anali kutsutsana naye, sanafune kusintha miyoyo yao. Anapitirilabe kutsatira miyambo yao. Tiyenera kumlola Yesu kukhala ndi njira yace m'miyoyo yathu. Tiyenera kulola ulamuliro wace kuti ulamulire miyoyo yathu.

## ZA INU

Kodi inu mumuganizira bwanji Yesu? Kodi inu mumutsata ndi kumvera? Pamene mumvera Yesu, anthu ena adzakutsutsani inu. Pamene mumvera Ambuye, mudzalandira mphotho.



Ndime 34. Pamene timulandira Yesu, timulola kuti alamulire miyoyo yathu. Tiyenera kutsata njira ya Yesu. Ngati ndi kotheka, tiyenera kudzunzidwa. Kudzikana mwini kutanthaudza osati kukhala m'mene tifunira ife eni. Kutanthauza kukhalira Yesu, ndi kumtsatira iye ndi njira yace.

Ndime 35. Pamene timulola Yesu kulamulira miyoyo yathu, amakhala mwa ife. Potaya miyoyo yathu m'njira imeneyi tiona cimene kukhala citanthaudza. Angakhale pamene tibvutika ndi Yesu kapena kumfera iye, timagawana m'moyo wace. Kutsatira Yesu kungatitengere miyoyo yathu.

Ndime 36-37. Tidzatsiriza ndalama zonse zimene tiri nazo, ndi kupemphanso zina, kuti tikhale ndi moyo. Tingakane kuonongelapo ndalama kuti tikhale bwino. Kodi ndalama zingaticitirenji ife ngati sitinakhale bwino?

Yesu anafunsa; Kodi dziko lonse liri ndi ciani ngati titaya mzimu wathu? Mzimu wathu uli wofunika koposa dziko lonse.

## ZA INU

Muganizira ciani za Yesu Kristu? Kodi mukhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu? Kodi munamulandira iye kukhala Mpulumutsi wanu?

Kodi Yesu Kristu m'mamuganizira bwanji? Muli okonzeka kumukhalira iye, angakhale mudzunzidwa kapena kufa?

## ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | |
|---|---|
| Lolemba: | 1 Mafumu 3:5-15 |
| Laciwiri: | 1 Mafumu 8:22-30 |
| Lacitatu: | 1 Mafumu 17:8-22 |
| Lacinai: | 1 Mafumu 18:17-21 |
| Lacisanu: | 1 Mafumu 19:1-12 |
| Loweluka | Luka 15:1-10 |
| Lamulungu: | Aroma 1:13-20 |

MARKO 8:31-33

*Ndipo anayamba kuwaphunzitsa, kuti kuyenera kuti Mwana wa munthu akamve zowawa zambiri, nakakanidwe ndi akuru ndi ansembe akuru, ndi alembi, nakaphedwe, ndipo mkuca wace akauke. Ndipo mauwo ananena poyera. Ndipo Petro anamtenga iye, nayamba kumdzudzula. Koma iye anapotoloka, napenya ophunzira ace, namdzudzula Petro, nanena, Coka, pita kumbuyo kwanga, Satana iwe' popeza susamalira zinthu za Mulungu, koma za anthu.*

Yesu anawaudza ophunzira kuti adzadzunzidwa. Adzakanidwa. Ndipo adzaphedwa. Koma adzauka kwa akufa.

Petro anakalipa. Sanafune kuganizira kuti Yesu ankanafa. Petro ndi ophunzira ena anali ndi zambiri zimene anafuna kuti Yesu adzicite. Anafuna kuti Yesu akhazikitse ulamuliro wa m'dziko. Kuzunzidwa ndi imfa inali njira yokhazikira ufumu wa Mulungu.

Yesu anati Petro anali kuona zinthuzi kudzera m'njira ya umunthu osati m'njira ya Mulungu. Yesu anamuitana Petro Satana cifukwa ca cimene anali kuganizira.

MPHOTHO YA KUTSATIRA YESU

Werengani zimene Yesu ananena kuti tiyenera kuzicita ngati tiri ophunzira.

MARKO 8:34-37

*Ndipo anadziitanira khamulo la anthu pamodzi ndi ophunzira ace, nati kwa iwo, Ngati munthu afuna kudza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wace, nanditsate ine. Pakuti yense wakufuna kupulumutsa moyo wace adzautaya; ndipo yense wakutaya moyo wace cifukwa ca ine, ndi cifukwa ca Uthenga Wabwino, adzaupulumutsa. Pakuti munthu apindulanji akadzilemezera dziko lonse, natayapo moyo wace? Pakuti munthu akapereka ciani cosintha naco moyo wace?*





# ANTHU SAMVETSETSA YESU

MAU A MULUNGU: Marko 3:7-35

MAU A PAMTIMA: *"Ndipo pamene abale ace anamva, anadza kudzamgwira Iye; pakuti anati adayaruka."*
*Marko 3:21*

CIDZIWITSO

Phunziro lathu sabata yatha linali la m'mene anthu anacitira pamene anakomana ndi Yesu. Anthu ambiri anamutsatira iye. Akuru akuru acipembedzo anatsutsana naye Yesu. Sanamvetse bwino iye.

Phunziro ili ndi la ena amene sanamvetsetse Yesu. Ophunzira ace sanamvetsetse Yesu (monga m'mene tidzaphunzirira mtsogolo). Angakhalenso banja lace silinamvetsetse iye.

ABWENZI A YESU SANAMUMVETSETSE IYE

Tiyeni tiwerenge ndimezi. Pezani cimene abwenzi ace anamuganizira iye.

MARKO 3:20-21

*Ndipo analowa m'nyumba. Ndipo anthu ambiri anasonkhananso, kotero kuti sanathe iwo konse kudya. Ndipo pamene abale ace anamva, anadza kudzamgwira Iye; pakuti anati adayaruka.*

Yesu adasiridza cabe kuitana ophunzira ace khumi ndi awiri (ndime 14-19). Anawaitana iwo kuti adzimuthandiza mu nchito yace ya kuciritsa, kulalikira, ndi kuturutsa mizimu yonyansa. Yesu ndi ophunzira ace anali ndi nchito yaikuru ndithu kuti analibe nthawi yodyera kapena yopumula.

Abwenzi a Yesu ndi banja lace anali wodankhawa ndi iye. Anaganizira kuti anali kugwira nchito kwambiri. Ena anaganiza kuti adayaruka. Sanaganizire kuti anthu adzamumvera iye. Anadziwa kuti a phunzitsi acipembedzo ca Ciyuda adzamuyambitsira mabvuto.

APHUNZITSI ACIPEMBEDZO SANAMVETSETSE YESU

Kodi aphunzitsi acipembedzo anacita ciani pamene Yesu anaturutsa mizimu yonyansa?

MARKO 3:22-27

*Ndipo alembi amene adatsika ku Yerusalemu ananena kuti, Ali naye Beelzibule, ndipo, Ndi mkuru wao wa ziwanda aturutsa ziwanda. Ndipo m'mene adawaitana iwo, ananena nao m'mafanizo, Satana angathe bwanji kuturutsa Satana? Ndipo ufumu ukagawanika pa uwu wokha, sukhoza kukhazikika. Ndipo nyumba ikagawanika pa iyo yokha, siikhoza kukhazikika nyumbayo, Ndipo Satana akadziukira mwini yekha, nagawanika, sakhoza kukhazikika, koma atsirizika. Komatu pali munthu akhoza kulowa m'nyumba ya mwini mphamvu, ndi kufunkha akatundu ace, koma athenge wamanga mwini mphamvuyo; ndipo pamenepo adzafunkha za m'nyumba mwace.*

Aphunzitsi acipembedza anali kunena kuti Satana anamupatsa mphamvu Yesu yoturutsira ziwanda ndi kuciritsira anthu. Anali kuganiza kuti Yesu anali kutumikira mphamvu ya Satana pocita zinthuzi.

Ndipo Yesu adati aphunzitsi acipembedzo sanali kuganizira bwino. Satana sakanakhoza kudziturutsa mwini wace. Ici citanthauza kuti Satana akanagawikana. Citanthauza kuti Satana akanadziononga iye mwini. Aphunzitsi anadziwa kuti Satana sangacite zotero.

Ndime 27 itiuza ife kuti Yesu anali ndi mphamvu pa Satana. Ici ndico cifukwa cace Yesu adali ndi mphamvu pa ziwanda. Pamene Yesu anaciritsa anthu amene anali wodzaza ndi



kukhala ndi zinthu zambiri za pa dziko lapansi pano ndipo kuti mzimu wathu utaike.

KOD' YESU NDANI?

Mu ndimezi werengani zimene anthu amaganizira za Yesu.

MARKO 8:27-30

*Ndipo anaturuka Yesu ndi ophunzira ace, nalowa ku midzi ya ku Kaisareya wa Filipi; ndipo panjira anafunsa ophunzira ace, nanena nao, Kodi anthu anena kuti ine ndine yani? Ndipo ananena, nati, Yohane Mbatizi; ndi ena, Eliya; koma ena, Mmodzi wa aneneri. Ndipo iye anawafunsa, Koma inu munena kuti ndine yani? Petro anayankha nanena naye, Ndinu Kristu. Ndipo anawauzitsa iwo kuti asanene kwa munthu mmodzi za iye.*

Tsiku lina Yesu anawafunsa ophunzira ace za m'mene anthu anali kuganizira za iye. Ophunzira anayankha. Anati anthu anali kuganiza kuti Yesu anali Yohane Mbatizi kapena m'neneri wa m'Cipangano Cakale akhalanso ndi moyo. Anthu ambiri sanadziwe amene Yesu anali.

Ndipo Yesu anawafunsa ophunzira za m'mene anaganizira kuti iye anali. Petro anayankha. Anati Yesu ndi Kristu (Mesiya).

Petro anapereka yankho lowona. Koma sanamvetsetse Yesu. Ici ndico cifukwa cace Yesu anawafunsira ophunzira ace kuti asanenere munthu ali yense za amene iye anali. Iwo panthawiyo anali wosaphunzitsidwa ndi kukonzeka kupitiriza nchito ya Yesu.

MTENGO WA KUOMBOLEDWA KWATHU

Tsopano werengani ndimezi. Kodi ophunzira anakondwera kumvera Yesu alinkunena za mabvuto ace?

MUTU 9

# KODI PAYENERA KUPEREKEDWA CIANI POOMBOLEDWA?

MAU A MULUNGU: Marko 8:27 mpaka 9:50

MAU A PAMTIMA: *"Ndipo anayamba kuwaphunzitsa, kuti kuyenera kuti Mwana wa munthu akamve zowawa zambiri, nakakanidwe ndi akuru ndi ansembe akuru, ndi alembi, nakaphedwe, ndipo mkuca wace akauke." Marko 8:31*

### CIDZIWITSO

Kuomboledwa kutanthauza kuti Yesu anapereka moyo wace cifukwa ca ife. Kodi tiganizira za mtengo wa kuomboledwa kwathu? Kodi tiganizira za kucuruka kwa zimene Yesu adazipereka kuti tiomboledwe?

Tiri ndi ufulu m'dziko lathu. Ici ndi cifukwa cakuti anthu amene analiko ife tisanabadwe anazunzidwa. Ena anafa ndipo ufulu wathu unaperekedwa pa miyoyo yao.

Phunziroli ndi ena ambiri amanena za kuzunzidwa ndi imfa ya Yesu. Uwu ndiwo mtengo wa kuomboledwa kwathu kapena kupulumuka.

### CIMENE PHUNZILORI LIMATIUZA IFE

(1) Zimene tiganizira za Yesu ndi zofunika. Osati ali munthu wabwino cabe amene anaphunzitsa coonadi ca Mulungu. Ndi mwana wa Mulungu.

(2) Yesu anazunzidwa ndipo anafa kuti atiombole ife. Yesu anapereka mtengo wapatali potiombola ife.

(3) Mzimu umodzi ndi wofunika kopambana zinthu zonse m'dziko lino lapansi. Ndikuputsa



ziwanda, anamugonjetsa Satana. Yesu ali ndi mphamvu kumposa Satana. Yesu angatithandize ife kumugonjetsa Satana m'miyoyo yathu.

### BANJA LA YESU SILINAMUMVETSETSE IYE

Ndimezi zinena za banja la Yesu limene silidamvetsetse iye.

### MARKO 3:31-35

*Ndipo anadza amace ndi abale ace naima kunja, namtumira uthenga kumuitana. Ndipo anthu ambiri anakhala pansi pomzinga; nanena kwa Iye, Onani, amanu ndi abale anu ali kunja akufunani Inu. Ndipo anawayankha nanena, Amai wanga ndi abale anga ndani? Ndipo anawaunguza-unguza iwo akumzingawo, nanena, Taonani, amai wanga ndi abale anga. Pakuti ali yense acita cifuniro ca Mulungu, yemweyo ndiye mbale wanga, ndi mlongo, ndi amai.*

Amai a Yesu ndi ena am'banjamo anali womudela nkhawa iye. Kapena anali kuganiza kuti Yesu adayaruka. Anafuna kupita naye kunyumba. Anafuna kumucotsa kwa anthu. Ndipo anamufunsa kuti apite ku nyumba. Yesu sanayankhe pamene banja lace linamuitana. Analikonda banja lace, koma anali ndi nchito yocita. Iwo sadamvetsetse kuti anali mwana wa Mulungu. Anafuna kucita nchito ya Mulungu.

Anthu ena anamuudza Yesu kuti banja lace limamufuna kuti apite kunyumba. Yesu anafunsa, "Banja langa kapena abale anga ndani?" Ndipo anayankhanso funsoli mwini wace. Kodi Yesu anati bwanji? Werenganinso ndime 35. Kodi inu muli amodzi a banja lace? Yesu anati kuti kucita cifuniro ca Mulungu ndiyo inali nchito yace. Iyinso ndiyo nchito yathu.

### ZA INU

Yesu afuna inu kuti mumukhulupirire ndi kumvera. Nthawi zina abwenzi anu ndi banja lanu sangamvetsetse pamene inu mucita zabwino. Kapena angatsutsanenso ndi inu.

Yesu adzakuthandizani inu kucita cifuniro ca Mulungu. Monga m'mene Yesu analiri ndi nchito yocita, Mulungu, ali ndi kanthu kena ka inu kamene muyenera kukacita. Mufunseni Mulungu kuti akuthandizeni kuti mucite nchito yanu.

### CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

(1) Anthu ambiri sadamvetsetse Yesu. Abwenzi ace ndi abale ace sadamuvetsetse iye. Aphunzitsi a lamulo sadamvetsetse Yesu. Anatsutsana naye.

(2) Yesu anapitirirabe kuciritsa anthu. Anapitirilabe kuphunzitsa ndi kulalikira. Ici cinali cifuniro ca Mulungu pa iye. Yesu anapitilila kugwira nchito pa zinthu zimene Mulungu adamupatsa kuti azicite.

(3) Sitimvetsetsa zonse zokhudza Mulungu ndi Yesu. Koma tidziwa kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu. Tingamukhulupirire iye monga Mpulumutsi wathu. Adzatipatsa mphamvu ndi cigonjetso pa Satana.

### ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | |
|---|---|
| Lolemba: | Ahebri 12:1-7 |
| Laciwiri: | Ahebri 13:7-17 |
| Lacitatu: | Yoswa 1:1-9 |
| Lacinai: | Yoswa 23:1-11 |
| Lacisanu: | Yoswa 24:14-24 |
| Loweluka: | Mateyu 10:34-39 |
| Lamulungu: | Deuteronomo 4:1-13 |



ziononga moyo zicokera ku mtima kapena ku maganizo. Maganizo oipa aononga.

### CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

(1) Cipembedzo ndi cofunika pamene zocita zathu ziri zoona. Zocita zathu, osati mau okha, zimasonyeza kuti timakonda Ambuye.

(2) Timamvera zocita zathu, osati ndi mau. Sitiyenera kulola miyambo kapena zizolowezi kutipanga ife anchito kwambiri kuti tilephere kucita nchito ya Mulungu.

(3) Miyoyo yathu imadetsedwa ndi zimene timaganizira ndipo zimene tinena. Tingakhale oyera pamene tikhala ndi maganizo abwino.

### ZA INU

Kodi cipembedzo canu ndi cofunika bwanji? Onani mayankho anu pocita zinthu zimene muzicita. Kodi mucita zinthu kamba ka cizolowezi? Ngati ziri tero, muli kutsatira mwambo.

Kodi mufuna kusintha ndi kucita bwino? Dzipatseni nokha mayeso awa. Yankhani inde kapena ai.

1. Kodi ndiwerenga Buku Lopatulika ndi kupemphera nthawi zonse?
2. Kodi ndimapita kukapemphera ku chalichi nthawi zonse?
3. Kodi ndi macitira umboni ndi kuthandiza anthu ena?
4. Kodi nditumikira Ambuye cifukwa cakuti ndi mkonda iye osati kudzisonyeza?

### ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | |
|---|---|
| Lolemba: | 1 Samueli 12:6-15 |
| Laciwiri: | 1 Samueli 15:10-23 |
| Lacitatu: | 1 Samueli 16:1-13 |
| Lacinai: | 1 Samueli 17:38-49 |
| Lacisanu: | 1 Samueli 26:12-23 |
| Lolweluka: | Mateyu 28:16-20 |
| Lamulungu: | 1 Samueli 7:8-18 |

masitolo, anali kusamba asanayambe kudya zimene anagula. Ici cinali cifukwa cakuti kapena munthu wina wakunja anacigwira cakudyaco. Panalinso miyambo yina imene Ayuda anali kuitsatira. Iye siinaphunzitsidwe m'Buku Lopatulika. Inali kupitilira cabe m'mibadwa yambiri mbiri (ndime 4).

Ophunzira analinso Ayuda. Bwanji sanatsatire mwambo wakusamba asanayambe kudya, Ayuda anafunsa (ndime 5).

MWAMBO WINA

Mu ndime 9-13 Yesu anapereka citsanzo cina ca m'mene Ayuda anali kutsatirira miyambo yao osati Buku Lopatulika. Buku Lopatulika likuti, "Lemekeza atate wako ndi amai wako" (Eksodo 2o:12). Ici citanthauza kuti tiyenera kuyang'anira makolo athu pamene iwo akalamba.

Yesu anati, "Bwanji mukaniza lamulo la Mulungu, kuti musunge mwambo wanu" (ndime 9). Ayuda anali ndi kanenedwe kakuti Korban.Cinali kutanthauza kuti munthu akanena kuti ali kupereka ndalama zace kwa Mulungu kapena ku Kacisi. Ndipo sankazigwiritsira nchito posungira makolo ace. Mwambowu siunacokere m'Buku Lopatulika.

KODI NDI CIANI CIMENE CIPANGITSA MUNTHU KUKHALA WODETSEDWA?

Werengani ndime 14-15. Yesu anadziwa kuti anthu anali kumvetsera ku zimene anali kunena Ayuda. Sankayenera kukhulupirira kuti miyambo inayenera kutsatiridwa.

Yesu ananena kwa anthu onse amene anali kumvetsera. Cimene ananena cinaperekanso yankho kwa Ayuda: "Kulibe kanthu kunja kwa munthu kakulowa mwa iye, kangathe kumdetsa, Koma zinthu zakuturuka mwa munthu, ndizo zakumdetsa munthu." (ndime 15)

Yesu anati kuti moyo wa munthu sungaonongeke ndi zinthu zimene akudya. Zinthu zimene





# KODI UFUMU WA MULUNGU NDI CIANI?

MAU A MULUNGU: Marko 4:1-34

MAU A PAMTIMA: *"Ndipo ananena, Tidzafanizira nji Ufumu wa Mulungu? kapena tidzaulinganiza ndi fanizo lotani? Ngati mbeu yampiru, imene ikafesedwa panthaka, ingakhale icepa ndi mbeu zonse za pdziko."*
*Marko 4:30-31*

CIDZIWITSO

Phunziro lathu loyamba linali la Yohane ndi Yesu ali kulalikira. Anawafunsa anthu kuti atembenuke ndi akonzekere ufumu wa Mulungu. Ufumu wa Mulungu, kodi Mulungu akhale m'miyoyo yathu. Pamene tapulumutsidwa ndi ticita cifuniro ca Mulungu, Mulungu akhala m'mitima yathu. Tiri mu Ufumu wa Mulungu.

Yesu anali kugwiritsa nchito zifanizo pophunzitsa zoonadi zokhudza Ufumu wa Mulungu. Zifanizo ndi nkhani imene itithandiza ife kumvetsetsa coonadi. Yesu anatithandiza ife kuti timvetsetse m'mene Ufumu wa Mulungu uliri.

CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

(1) Tiyenera kusonyeza ena za coonadi ca Mulungu. Miyoyo yathu iyenera kusonyeza kuti Mulungu akukhala m'mitima yathu.

(2) Tiyenera kumvera kwa Mulungu ndi tigwiritse nchito cikhulupiriro cimene atipatsa. ife. Tikatero tidzaphunzira zambiri. Tidzamvetsetsa kwambiri za coonadi ca Mulungu.

(3) Pamene coonadi cadzalidwa m'miyoyo yathu. cidzakula. Mulungu alonjeza kuti coonadi cidzakula ndipo cidzakhala ndi zipatso m'miyoyo yathu.

*Ndipo ananena ndi iwo, kodi atenga nyali kuti akaibvundikire mbiya, kapena akaiike pansi pa kama, osati kuti akaiike pa coikapo cace? Pakuti kulibe kanthu kosisika, koma kuti kaonetsedwe; kapena kulibe kanthu kanakhala kam'tseri, koma kuti kakaululidwe. Ngati munthu ali nao makutu akumva, amve. Ndipo ananena nao, Yang'anirani cimene mukumva; ndi muyeso umene muyesera nao udzayesedwa kwa inu; ndipo kudzaonjezedwa kwa inu. Pakuti kwa iye amene ali nako kanthu, kadzapatsidwa; ndipo kwa iye amene alibe kanthu, kadzacotsedwa ngakhale kanthu kali konse ali nako.*

Munthawi ya Yesu nyumba zinali ndi cipinda cimodzi basi. Anthu amawika nyali pa guwa la miyala pa phambo. Nyali imaunika m'cipinda conse. Pamene tifuna kuwerenga mabuku athu, timakoleza nyali zathu ndipo timaziika pa ma gome.

Ife Akristu tiyenera kuonetsa nyali ya Mulungu ilikuwala m'miyoyo yathu kwa anthu ena. Tiyenera kunena zoona za ufumu wa Mulungu: Ena adzamudziwa Mulungu. Ufumu wace udzabwera m'miyoyo yao (ndime 22).

Ambuye ali kuyitana anthu onse kuti amvetsere ku coonadi cace ca ufumu wace (ndime 23). Ena amakhulupirira. Koma ena sakhulupirira coonadi ca Mulungu. Samvera ndi kutsatira Ambuye.

Pamene timvera ndi kumvera tiphunzira zambiri. Tiyenera kugwiritsa nchito cikhulupiriro cathu. Ndipo kumvetsetsa kwathu kudzapitirira. "Onani kuti mucita zimene mukuzimva. Ngati mucita tero nthawi zambiri, muzamvetsetsadi zimene ndikuuzani."

Pamene tigawana ndi ena ufumu wa Mulungu, kumvetsetsa kwathu kukula. Ngati tigawana ndi ena cikhulupiriro cathu, cikhulupiriro cathu cidzakulanso. Tiyenera kupitiriza kucitira umboni wa Ambuye.



*mkate wao ndi m'manja mwakuda? Ndipo iye ananena nao, Yesaya ananenera bwino za inu onyenga, monga mwalembedwa, Anthuwa andilemekeza ine ndi milomo yao, Koma mtima wao ukhala kutari ndi ine. Koma andilambira ine kwacabe, ndi kuphunzitsa maphunzitso, malangizo a anthu. Musiya lamulo la Mulungu, nimusunga mwambo wa anthu. Ndipo ananena nao, Bwino mukaniza lamulo la Mulungu, kuti musunge mwambo wanu. Pakuti Mose anati, Lemekeza atate wako ndi amako; ndipo iye wakunenera zoipa atate wace kapena amai wace, afe ndithu; koma inu munena, Munthu akati kwa atate wace, kapena amai wace, Korban, ndiko kuti Mtulo, cimene ukadathandizidwa naco ndi ine, simulolanso kumcitira kanthu atate wace kapena amai wace; muyesa acabe mau a Mulungu mwa mwambo wanu, umene munaupereka: ndi zinthu zotere zambiri muzicita. Ndipo anadziitaniranso khamu la anthu, nanena nao, Mverani ine nonsenu, ndipo dziwitsani: kulibe kanthu kunja kwa munthu kakulowa mwa iye, kangathe kumdetsa: koma zinthu zakuturuka mwa munthu ndizo zakumdetsa munthu.*

## KUTSATIRA MWAMBO

Taonaninso ndime 1-5. Afarisi ndi alembi anali aphunzitsi acipembedzo caciyuda. Sanabwerere kudzamvetsera kwa Yesu ndi kumtsatira iye. Anabwera kudzaonapo cifukwa ndi Yesu (ndime 1).

Atsogoleri acipembedzo anacipedza cifukwa ndi ophunzira a Yesu. Anaona kuti ophunzira sanali kusamba asanayambe kudya (ndime 2).

Unali mwambo wa Yuda kusamba m'manja, sikunali kuti manja awo akhale oyera. Cinali kucitika monga mwambo.

Ayuda sankanadya kufikira atasamba manja awo kufikira m'zigongo. Anakhala ali kucita izi pa zaka zambiri. Iwo anali kuonetsetsa kuti sanasiye.

Pamene Ayuda anali kubwera kucokera ku

# PAMENE CIPEMBEDZO NDI COFUNIKA

MAU A MULUNGU: Marko 7:1 mpaka 8:26

MAU A PAMTIMA: *"..Anthu awa andilemekeza Ine ndi milimo yao, koma mtima wao ukhala kutari ndi ine. Koma andilambira ine kwacabe ndi kuphunzira maphunzitso, malangizo a anthu."*
*Marko 7:6-7*

CIDZIWITSO

Kufunika citanthauza cinthu cimene munthu angatumikire, kapena cinthu cimene munthu sangagwire bwino nchito ngati ico palibe.

Pamene cipembedzo ndi cofunika, timamutumikira Mulungu cifukwa timukonda iye. Sitimayesa kudzionetsa kwa ena.

Phunziro ili ndi la ciphunzitso ca Yesu pa cipembedzo cimene ndi cofunika. Mu ndimezi pezani (1) zimene Yesu ananena zokhudza kutsatira mwambo yakale, ndi (2) zimene Yesu ananena kuti zimadetsa munthu.

MARKO 7:1-15

*Ndipo anasonkhana kwa iye Afarisi, ndi alembi ena, akucokera ku Yerusalemu, ndipo anaona kuti ophunzira ace ena anadya mkate ndi m'manja mwakuda, ndiwo osasamba. Pakuti Afarisi, ndi Ayuda onse sakudya osasamba m'manja ao, kuti asungire mwambo wa akuru; ndipo pakucoka kumsika, sakudya osasamba m'thupi; ndipo ziripo zinthu zina zambiri anazilandira kuzisunga, ndizo matsukidwe a zikho, ndi miphika, ndi zotengera zakumwa. Ndipo Afarisi ndi alembi anamfunsa iye, kuti, Bwanji ophunzira anu satsata mwambo wa akuru, koma akudya*





Tsopano werengani ndimezi. Pezani m'mene ufumu wa Mulungu uliri monga mbeu.

MARKO 4:26-29

*Ndipo ananena, Ufumu wa Mulungu uli wotero monga ngati munthu akataya mbeu panthaka; nakagona ndi kuuka usiku ndi usana, ndipo mbeu zikamera, ndi kukula, iye sadziwa umo zicitira. Nthaka ibala zipatso zace yokha; uyamba mmera, zitsata ngala, pamenepo maso okhwima m'ngalamo pakucha zipatso, pamenepo atumiza zenga, pakuti nthawi yakumweta yafika.*

Pamene tibzala mbeu za dzungu, tiona kuti posacedwa zayamba kumera. Tsiku liri lonse tiona kuti mbeuzo zikukulabe. Ndipo zipatso zace zazing'ono (dzungu) ziyamba kumera. Sitingazione zilinkumera kapena kuzimvera zirinkumera. Koma tidziwa kuti zilinkumera.

Yesu anagwiritsa nchito cifanizo cimeneci ca mbeu. Alimi adziwa kuti mbeu ziyenera kubzalidwa. Mbeuzo ziri kufuna madzi m'nthakamo. Posacedwa cimanga kapena tirigu aturukira. Mulungu anali kugwira nchito kacetecete mu mbeuzo ndi zomera zace ndiponso ndi zipatso zace. Sitingadzimve zinthu zimenezi. Tidziwa kuti ziri kucitika. Cipatso ndico cinthu cotsimikidzira.

Pamene ufumu wa Mulungu uli kugwira nchito m'miyoyo yathu, anthu aona zipatso zace. Miyoyo yathu iwonetsa pamene tibvomereza kuti coonadi ca Mulungu cilamulire m'miyoyo yathu. Anthu angadziwe kuti zinthu zabwino zikugwira nchito m'miyoyo yathu.

UFUMU ULI MONGA MBEU YA MPIRU

Werengani fanizoli kuti muone m'mene ufumu wa Mulungu umakulira.

## MARKO 4:30-32

*Ndipo ananena, Tidzafanizirànji Ufumu wa Mulungu? kapena tidzaulinganiza ndi fanizo lotani? Ngati mbeu yampiru, imene ikafesedwa panthaka, ingakhale icepa ndi mbeu zonse za padziko, koma pamene ifesedwa, imera nikula koposa zitsamba zonse, nicita nthambi zacikuru; kotero kuti mbalame za m'mlengalenga zikhoza kubindikira mumthundi mwace.*

Mbeu ya mpiru monga imene idaliko panthawi ya Yesu, inali yaying'ono kwambiri. Koma inapanga mtengo waukulu. Mbalame zinakhoza kupanga nyumba zawo m'menemo m'nthambi zace.

Yesu anati ufumu wa Mulungu unali monga mbeu ya mpiru. Amatanthaudza kuti zoona za ufumu zimayamba zazing'ono. Koma zizakula m'miyoyo yathu. Zinthu zambiri zimayamba zazing'ono. Cikhulupiriro cathu cingayambe cacing'ono. Cimakula pamene timvomereza Mulungu kugwira nchito m'miyoyo yathu. Zoonadi zace ziyenera kulamulira mumitima yathu. Mulungu akuti ufumu wace udzakula m'miyoyo yathu.

### ZA INU

(1) Pangani kuti coonadi ca Mulungu cidzale m'moyo wanu. Pangani kuti coonadi cace cigwire nchito m'miyoyo yanu.

(2) Muonetseni munthu wina cimene Mulungu akucitirani inu. Tamuuzani iye za m'mene munapulumutsidwira. Iyi ndiyo njira pogawana ufumu wa Mulungu ndi anthu ena.

### ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | | |
|---|---|---|
| Lolemba: | Deutoronomo | 6:3-15 |
| Laciwiri: | Deutoronomo | 7:1-13 |
| Lacitatu: | Deutoronomo | 11:13-25 |
| Lacinai: | Deutoronomo | 26:1-11 |
| Lacisanu: | Deutoronomo | 30:12-20 |
| Loweluka: | Mateyu | 13:18-23 |
| Lamulungu: | Deutoronomo | 32:1-10 |



pa gombe. Kodi mungawerenge mutu wonsewo kuti mupeze cimene cinacitika?

### CIMENE PHUNZILORI LIMATIUZA IFE

(1) Ophunzira oyamba a Yesu anali kucita nchito imodzi modzi ndi imene Yesu anali kucita. Anawapatsa mphamvu. Ife tiri ophunzira ace ndipo tiyenera kucita nchito yace.

(2) Tiyenera kukhala ndi makhalidwe abwino kuti ticite nchito ya Ambuye. Tiyenera kucitabe zinthu zimene Ambuye anatiitanira kuti tidzicite.

(3) Pamene Ambuye atipatsa ife nchito kuti ticite, atipatsanso mphamvu yocitira nchitoyo.

### ZA INU

Ngati muli Akristu, muli ophunzira a Yesu.

Kumbukirani zinthu izi:

Mungacitire umboni ndi kutumikira ena.
Mungakhale ndi makhalidwe abwino kuti mucite bwino nchito yanu.
Muyenera kupitirilabe kugwirira nchito Ambuye m'nchito imene muli nayo.
Ambuye adzakuthandizani inu kuti mugwire nchito imene afuna kuti mugwire.
Ambuye adzakupatsani inu mphamvu.

### ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | | |
|---|---|---|
| Lolemba: | 1 Akorinto | 9:13-23 |
| Laciwiri: | 1 Akorinto | 10:23-33 |
| Lacitatu: | 1 Akorinto | 11:23-34 |
| Lacinai: | 1 Akorinto | 12:14-27 |
| Lacisanu | 1 Akorinto | 13:1-13 |
| Loweluka | Mateyu | 25:31-40 |
| Lamulungu | 1 Samueli | 3:1-10 |

uthenga umodzi modzi umene Yesu anali kulalikira. Anawafunsa anthu kutembenuka ku ucimo.

Ophunzira anaturutsa mizimu yonyansa. Anaciritsa anthu odwala. Izi ndi njira zimene Yesu anacita kuti mphamvu yace ithandize anthu. Yesu anawapatsa ophunzira ace mphamvu kucita zinthuzo ndi kuthandiza anthu.

Werengani ndimezi kuti muone zimene Yesu anawatuma ophunzira ace kuti acite.

MARKO 6:30-34

*Ndipo atumwi anasonkhana kwa Yesu; namuuza ziri zonse adazicita, ndi zonse adaziphunzitsa. Ndipo Iye ananena nao, Idzani inu nokha padera ku malo acipululu, mupumule kamphindi. Pakuti akudza ndi akucoka anali piringu piringu, ndipo analibe nthawi yokwanira kudya. Ndipo anacokera m'ngalawa kunka ku malo acipululu padera. Ndipo anthu anawaona alikumuka, ndipo ambiri anawazindikira, nathamangira limodzi kumeneko pamtunda, ocokera m'midzi monse, nawapitirira. Ndipo anaturuka Iye, naona khamu lalikuru la anthu, nagwidwa cifundo ndi iwo, cifukwa anali ngati nkhosa zopanda mbusa; ndipo anayamba kuwaphunzitsa zinthu zambiri.*

Ndime 31. Yesu anadziwa kuti anali wotopa. Onse anali ndi nchito kwambiri kuti analephera ndi kudya komwe. Anawafunsa kuti apume. Anafuna nthawi yokhalira ndi Yesu. Ifenso timafuna kupumula ku nchito yathu ndi kupembedza Mulungu.

Ndime 32-33. Yesu ndi ophunzira ace anayetsa kucokako kwa anthu kuti akapumule. Analowa m'ngalawa. Anthu anali kuwathamangirabe. Anthu anathamanga modzungulira nyanja nakomana ndi Yesu ndi ophunzira ace ku mbali ina.

Ndime 34. Pamene Yesu anawona anthu, anawacitira cifundo. Anali kufuna iye. Panalibe nthawi kuti iye apumule. Ndipo Yesu anayamba kulankhula naonso anthuwo. Anawaphunzitsa iwo





# MPHAMVU YAIKURU YA YESU

MAU A MULUNGU: Marko 4:35 mpaka 6:6

MAU A PAMTIMA: *"Ndipo iwo anacita mantha akuru, nanenana wina ndi mnzace, Uyu ndani nanga, kuti ingakhale mphepo ndi nyanja zimvera Iye?"*
*Marko 4:41*

## CIDZIWITSO

Phunziro lathu lapitali linali la Yesu alinkuphunzitsa ndi zifaniziro. Anagwiritsa nchito zifaniziro pophunzitsa zoonadi za ufumu wa Mulungu.

Phunziro ili linena za mphamvu ya Yesu pa namondwe. Namondwe anali mu nyanja. Anagwiritsanso nchito yace kuciritsa munthu odwala. Kodi mumakumbikira maphunziro a 3 ndi 4 pamene Yesu anali kuciritsa anthu odwala?

Yesu anali ndi mphamvu yaikuru. Sanadzikuze ndi mphamvu zace. Mulungu anamupatsa iye mphamvu. Iye anagwiritsa nchito mphamvuzo pothandizira anthu.

## CIMENE PHUNZIROLI LIMATIUZA IFE

(1) Yesu ali ndi cidwi ndi miyoyo yathu. Afuna kutithandiza ife kukhala cete. Ndipo tidzakhala ndi mtendere m'miyoyo yathu.

(2) Tiyenera kukhala ndi cikhulupiriro mu mphamvu za Yesu potithandiza ife. Adzatikhulululukira macimo athu. Yesu adzatithandiza ife kukhala monga m'mene iye afunira kuti tikhalire.

(3) Yesu afuna kutithandiza ife pamene tadwala kapena pamene tiri m'mabvuto. Adzati-

patsa mphamvu ndi cigonjetso pamene nthenda ndi mabvuto zibwera.

## YESU ANAGWIRITSA NCHITO MPHAMVU YACE M'NAMONDWE

Werengani m'mene Yesu anagwiritsira nchito mphamvu yace yaikuru kuthandiza anthu ena amene anali m'mabvuto.

MARKO 4:35-41

*Ndipo dzuwa lomwelo, pofika madzulo, ananena kwa iwo, Tiolokere tsidya lina. Ndipo posiya khamulo anamtenga apite nao, monga momwe anali, mungalawa. Ndipo panali ngalawa zina pamodzi ndi iye. Ndipo panauka namondwe wa mkuru wa mphepo, ndi mafunde anagabvira mungalawa, motero kuti ngalawa inayamba kudzala. Ndipo iye mwini anali kutsigiro, nagona tulo pamtsamiro; ndipo anamuutsa Iye nanena kwa Iye Mphunzitsi, kodi simusamala kuti titayika ife? Ndipo anauka, nadzudzula mphepo, nati kwa nyanja, kuti, Tonthola, khala bata. Ndipo mphepo inaleka, Ndipo, kunagwa bata lalikuru. Ndipo ananena nao, Mucitiranji mantha? kufikira tsopano mulibe cikhulupiriro kodi? Ndipo iwo anacita mantha akuru, nanenana wina ndi mnzace, Uyu ndani nanga, kuti ingakhale mphepo ndi nyanja zimvera Iye?*

Yesu anakhala alikulalikira ndi kuthandiza anthu tsiku lonselo. Iye ndi ophunzira ace analowa m'ngalawa kuti apite kutsidya kwa nyanja ya Galileya. Yesu anali wotopa kwambiri. Anafuna kuusiya unyinji wa anthu kuti akapumule. Posacedwa anagona.

Namondwe anayamba kuyiomba ngalawayo. Mafunde akuru ndithu anathira madzi m'ngalawamo. Ophunzira ace anadziwa m'mene namondwe amayipira pa nyanja ya Galileya. Anaganiza kuti kapena ngalawa ingamire.

Ophunzira ace anaganizira kuti sanali ndi nkhawa ndi cimene cikanacitika kwa iwo cifukwa iye anali cigonere. Anamuutsa Yesu



*pamalo ponse sakulandirani, kapena kumvera inu, pakucoka kumeneko, sansani pfumbi liri ku mapazi anu, likhale mboni ya kwa iwo. Ndipo anaturuka nalalikira kuti anthu atembenuke mitima. Ndipo anaturutsa mizimu yoipa yambiri, nadzoza mafuta anthu ambiri akudwala, nawaciritsa.*

Ndime 7. Yesu anaitana anthu khumi ndi awiri kuti amuthandize iye. Anali ophunzira ace oyamba. (Mungawachule maina awo? Ngati simungathe, (Werengani Luka 6:13-16). Yesu anawatumiza anthu khumi ndi awiriwo, mogawikana awiri awiri. Anawapatsa mphamvu pa ziwanda.

Ndime 8-9. Yesu anawafunsa ophunzira kuti asatengenso zinthu zina za padera pa ulendowo. Ankayenera kutenga zokhazo zimene anali kudzifuna: ndodo, nsapato, ndi sutu imodzi ya cobvala. Sankayenera kutenga cikwama, ndalama, kapena cakudya.

Ndime 10. Anthu anali kuwapatsa a paulendo malo ogonapo ndi cakudya. Yesu anawafunsa ophunzira kukakhala pamene anaitanidwa. Sanayenera kuyenda nyumba ndi nyumba. Anayenera kukhala m'nyumba imodzi usiku uli onse kufikira atacokeramo mu tauniyo.

Ndime 11. Ngati matauni Aciyuda sanawalandire ophunzira; kapena kumvera uthenga wao, ophunzira sanayenera kukhala. Pamene analinkupita ophunzira anayenera kunsasa dothi lakumapazi awo. Uwo unali mwambo. Cinatanthauza kuti ophunzira sankalalikiraponso pa malopo. Anapita kukalalikira kwa anthu amene anali wokonzeka kumvera.

Sodomo ndi Gomora anaonongeka ndi moto cifukwa anali malo aucimo kwambiri (Genesis 19:24-25).

Yesu anati zikanaipa kwa matauni amene sankafuna kumvera uthenga wa ophunzira.

Ndime 12-13. Kodi munalembako mizere kunsi kwa mau amenewa? Ophunzira analalikira

*ambiri, nalipira zonse anali nazo, osacira pang'ono ponse, koma makamaka nthenda yace idakula, m'mene iye anamva mbiri yace ya Yesu, anadza m'khamu kumbuyo kwace, nakhudza cobvala cace. Pakuti ananena iye, ngati ndikakhudza ngakhale zobvala zace ndidzapulumutsidwa. Ndipo pomwepo kasupe wa nthenda yace adaphwa; ndipo anazindikira m'thupi kuti anaciritsidwa cibvutiko cace. Ndipo anati kwa iye, Mwana wamkaziwe, cikhulupiriro cako cakupulumutsa; muka mumtendere, nukhale wocira cibvutiko cako.*

Yesu pamenepa anali kupita ku nyumba ya Yairo. Mwana wa mkazi wa Yairo anali odwala. Anamufunsa Yesu kuti apite nakamuciritse mwanayo. (Werengani ndime 21-24, 35-43).

Khamu la anthu linali kumutsatira iye pamene anali kupita ku nyumba ya Yairo. Mkazi m'khamulo anali alinkudwala kokwanira zaka khumi ndi ziwiri. Thupi lace silinkaleka kucoka mwazi.

Mkaziyo anakhulupirira kuti Yesu akanamuciritsa iye. Panali ciunyinji ca anthu, ndipo sanathe kumuona Yesu. Ngati akanakhudza cabe zobvala zace, anakhulupirira kuti akanakhala bwino. Posacedwa anamuyandikira Yesu. Anawakhudza malaya ace. Mwazi unaleka kuturuka pomwepo. Anali bwino.

Yesu anadziwa kuti munthu wina anamugwira iye. Anafunsa kuti anali ndani kawiri. Mkaziyo anamuuza cimene cidacitika (ndime 30-33). Yesu anati anali ndi cikhulupiriro cacikuru. Anali wokondwa cifukwa cikhulupiriro cace anacigwiritsira nchito. Kodi mukumbukira cimene Yesu ananena kwa ophunzira ace atapangitsa nyanja kukhala cete? Werenganinso Marko 4:40.

## ZA INU

Kodi mumafunsapo Ambuye kumuthandizani inu kuti mucite kanthu kena? Afuna inu kuti



muwaitane. Musacite mantha kapena manyazi powaitana.

Ngati simuli Akristu, Ambuye afuna kuti mupulumutsidwe. Iwo alinso ndi cidwi ndi nchito yanu, moyo wanu, ndiponso banja lanu. Pempherani kwa iye za zinthu zonsezi.

## ZOWERENGA MASIKU ONSE

| | |
|---|---|
| Lolemba: | Oweruza 7:1-9 |
| Laciwiri: | 1 Akorinto 1:18-31 |
| Lacitatu: | 1 Akorinto 2:1-10 |
| Lacinai: | 1 Akorinto 3:9-17 |
| Lacisanu: | 1 Akorinto 4:1-14 |
| Laciwelu: | Mateyu 18:21-35 |

MUTU 7

# MAKHALIDWE ABWINO A OPHUNZIRA

MAU A MULUNGU: Marko 6:7-56

MAU A PAMTIMA: *"Tiyenera kugwira nchito za Iye wonditumo Ine, pokhala pali msana; ukudza usiku pamene palibe munthu angakhoze kugwira nchito."*
*Yohane 9:4*

## CIDZIWITSO

Makhalidwe abwino atanthauza kudziletsa. Ophunzira ndi munthu amene aphunzira kwa wina. Tiyenera kukhala ndi makhalidwe abwino m'miyoyo yathu pophunzira zinthu zatsopano ndi kutsatira citsanzo ca Yesu. Tiyeneranso kutumikira ndi kucitira umboni kwa anthu ena.

Phunziroli linena za nthawi imene Yesu anaitanira ophunzira ace khumi ndi awiri, pambuyo pace ochedwa atumwi. Anawafunsa iwo kulalikira, kuphunzitsa, kuciritsa, ndi kuturutsa ziwanda. Anawapatsa mphamvu kucita zinthu zimenezi.

Mu ndimezi lembani mizera kunsi kwa zinthu zimene Yesu anawafunsa ophunzira ace kuti adzicite.

MARKO 6:7-13

*Ndipo anadziitanira khumi ndi awiriwo, nayamba kuwatumiza iwo awiri awiri; nawapatsa mphamvu pa mizimu yonyansa; ndipo anawauza kuti asatenge kanthu ka paulendo, koma ndodo yokha; asatenge mkate, kapena thumba, kapena ndalama m'lamba lao; koma abvale nsapato; ndipo anati, Musabvale malaya awiri. Ndipo ananena nao, Kumene kuli konse mukalowa m'nyumba, khalani komweko kufikira mukacokako. Ndipo*



namufunsa, "Mphunzitsi, kodi simusamala kuti titayika ife?" (ndime 38)

Yesu analankhula kwa namondwe. Mphepo inasiya kuomba. Madzi anakhala cete. Mafunde anasiya kupindimuka. Nyanja inalinso bwino bwino.

Ndipo Yesu analankhula kwa ophunzira ace. Iye anakhumudwa ndi iwo. Anawafunsa kuti n'cifukwa ciani analibe cikhulupiriro mwa iye. Ngati anali ndi cikhulupiriro mwa iye, sakanakhala ndi mantha.

Ophunzira ace anali kumuona Yesu pamene anali kuciritsa anthu odwala. Anamuona iye alinkuturutsa ziwanda. Tsopano anamuona alinkugonetsa namondwe. Anadabwa kuti anali ndi mphamvu yotere. Werengani ndime 41 (mau athu a pamtima). Kodi muganiza kuti ophunzira anamukhulupirira Yesu tsopano kuti anali kuwasamala iwo? Kodi anayamba kukhala ndi cikhulupiriro cacikuru mwa iye?

Yesu anagwiritsa nchito mphamvu yace kuwathandizira ophunzira ace. Anacotsa mantha amene anali nawo. Anamondwe a mtundu wina amabwera m'miyoyo yathu. Bvuto lingakhale monga namondwe. Ife tiri ndi mantha cifukwa ca zinthu zimene zicitika. Yesu akhoza kuthetsa namondwe woteroyo. Iye sangacotse bvuto. Koma adzatipatsa mphamvu. Ndipo tingagonjetse bvutolo ndi namondweyo m'miyoyo yathu.

## YESU ANAGWIRITSA NCHITO MPHAMVU YACE POCIRITSA

Werengani m'mene Yesu anagwiritsira nchito mphamvu yace kuciritsa munthu amene anali ndi cikhulupiriro mwa iye.

MARKO 5:25-29 ndi 34

*Ndipo munthu wamkazi amene anali ndi nthenda yacidwalire zaka khumi ndi ziwiri, ndipo anamva zowawa zambiri ndi asing'anga*